# *MUWOMBOLI WACHIBALE*

Zikomo inu, M'bale Neville. Ambuye akudalitseni. Nchabwino kwambiri kuti tabwereranso kachiwiri, mmawa uno, kubwerera mnyumba ya Ambuye. Ine ndikukhulupirira zinanenedwapo, nthawi yina, "Ine ndinali wokondwa pamene anati kwa ine, 'Tiyeni tipite kunyumba ya Ambuye.'"

Charlie, choka kuseri kwa nsanamira imeneyo, ndipo ubwere pamtunda pano ndipo udzadzipezere mpando. Tabwera pamtunda pano. Mlongo, kodi kuli mpando kumbuyo uko, penapake, umene tingathe kuwupezera malo? Apa pali malo pomwe *apa*, dona. Tabwera komwe kuno apa. Apa, Charlie, tabwera kuno ndipo udzakhale pansi pafupi ndi Banks pomwe apa, kuchitira kuti usachite kuimirira. Nthawi iliyonse mnyamata ameneyo akabwera kuchokera kutali ku Kentucky, akafika kuno, iye amaimirira, mmawa uliwonse. Ndipo ife timukhazika iye pomwe apa.

2 Apa pali malo apa, kumapeto kwa mpando apa, a winawake. [M'bale Neville akuti, "Pali dona kumbuyo kuno, aponso."—Mkonzi]. Pali dona waimirira kumbuyoko, kumbuyo uko. Bwerani komwe kuno. Apa pali mpando cha apa, mlongo, pafupi kwambiri. Kazibwerani kutsogolo kuno. Ndipo ine ndikuganiza winawake ali mu chikuku apo. Kodi iwo ali? [Mlongo akuti, "M'bale Branham?"] Inde. ["Pali mpando pomwe apa."] Pali mpando wina cha pomwe *apa*. Ngati winawake akuwufuna wina, kumbuyo uko mmbuyo, pomwe *apa* pali mpando pomwe apa. [M'bale akuti, "Ndipo apa pali umodzi, M'bale Branham."] Apa pali umodzi pomwe apa, apanso, mungopanga zoti zikuthandizeni. ["Umodzi wina, cha apa."] Inde. Inu mukhoza kukhala ndi umodzi pomwe apa. Tsopano, kazibwerani, khalani mmipando yanu. Ndipo mungomverera kwenikweni . . .

3 Tikufuna kuti inu mukhazikike pamene tikuyesetsa kuti tibweretse Mawu a Ambuye. Oh, ndithudi ndi chabwino kukhala pano.

4 Ine sindinamuwone Charlie pa nsanja. Kodi iye ali kumbuyo uko? Chabwino, m'bweretsani iye kuno. Mai! Ine ndakhala ndiri ndi Charlie, kumusi uko, masiku angapo apitawa, ndipo ine sindingathe kudutsa opanda kupita ku nyumba kwake ndi kukadya, chotero ine ndimubweretsa iye pa nsanjapa, mmawa uno. Tsiku lirilonse iye akabwera kuno, iye amayima mozungulira khoma apo, kuti amupatse winawake pokhala. Chotero ine ndinayang'ana kunja mmawa uno ndipo ine ndinadzamuwona iye atayima pamenepo, ine ndinaganiza, "Ine ndi—ine ndimulowetsa iye muno tsopano." Chabwino, ziri—

ziri bwino. Tsopano ife tikhala ndi uthenga m'mawa uno wolalikidwa ndi M'bale Russell Cox. [M'bale Branham ndi osonkhana akuseka—Mkonzi]. Kodi Nellie ali kuti? Ine... Umenewo udzakhala ulendo wabwino kwa iye. Kuti? Eya. Ndi zimenezotu.

5 Chabwino, ndine wokondwa ndithudi kuwona ochuluka a abwenzi atatuluka. Lamlungu lapitali nditachoka, ine ndinamverera moyipa sabata yonse. Ine ndinali ndi mzanga wabwino wakhala apa, wochokera kutali komwe Kummwera, M'bale West. Ndipo ine ndinali nditazungulira, kudutsa mwa omvetsera, mochedwa. Ine ndinati, "Ndine wokondwa kumuwona *Wakuti-ndi-wakuti* ndi *Wakuti-ndi-wakuti*," ndipo ine ndinayang'ana kudutsa pamwamba pa M'bale West, ndipo sindinati—sindinamuzindikire konse iye mpaka iye atayamba kumatuluka. Ndiye ine ndinaganiza, sabata yonseyi, "M'bale West aziganiza kuti ine—ine basi ndinangofuna kuti ndimudutse iye." Koma iye—iye ndi Mkhristu, chotero iye akudziwa bwinoko kuposa zimenezo. Iye akudziwa kuti ine...bwenzi lenileni. Ndipo ine ndikudziwa kuti iye amadziwa, ine sindingachite zimenezo.

6 Ine ndimaganiza mmawa uno, ndikubwera kuno, powawona anthu amene abwera kuchokera ku malo osiyanasiyana. Tsopano, apa pali M'bale West abwereranso kuno kachiwiri, mmawa uno. Ndi M'bale ndi Mlongo Kidd pano, ochokera ku Ohio. Ndi ena a anga...

Ine ndikudziwa M'bale Evans ali pano. Ine ndinapita kukamuwona iye, dzulo masana, ku motelo, koma ndikuganiza iye anatuluka ndi M'bale Fred ndi iwo. Ndipo iwo amabwera njira yonse kuchokera ku Macon, Georgia, kuno, Lamlungu lirilonse limene ine ndikuyankhula. Kuchokera ku Macon, Georgia, umenewo ndi mtunda wautali kumusi uko. Iwo ndi pafupifupi mailosi eyiti handirede, kapena kuposerapo, ine ndikuganiza, kumusi uko. Amayendetsa ndi banja lake, tsiku lirilonse limene ine ndikuyankhula. Ndipo kumeneko ndi kukhulupirika.

7 Ndipo ine ndima—ndimaganiza, oh, ndiye, ngati iwe ukhala ndi abwenzi ngati amenewo, amene amafuna kuti aziyima pafupi ndi iwe! Tsopano, izo...anthu amenewo samabwera njira yonse kuchokera ku Georgia, ndi Ohio, ndi madera osiyanasiyana a fukoli, kubwera ku kachisi wamng'ono uyu pano, kuti adzandimve ine. Iwo amabwera kuno chifukwa iwo amawukhulupirira Uthenga umenewo. Ndi zimene iwo amakhulupirira. Iwo akuwukhulupirira Uthenga umenewo. Ndiyeno ine ndikuyenera kukhala woonamtima ndi wodzipereka bwanji pa Uthenga umenewo! Chifukwa, osati—osangoti inemwini, ine ndikulakwitsa, koma ine ndikumutsogolera winawake molakwika. Mukuona? Ndiyeno Mulungu adzandiimba ine mlandu chifukwa cha kulakwitsa

kwawoko, chifukwa ine ndi amene ndinawaphunzitsa zimenezo. Mukuona?

8 Ndipo ine ndikukuuzani inu, zimenezo ndithudi zimakupangitsa iwe kuganiza mwakuya pamene iwe uyamba kuganiza za zinthu monga zimenezo. Chotero ine—ine ndikuyamikira aliyense wa inu, nzabwino kwambiri kudziwa kuti mukumayendetsa mahandiredi a mamailosi amenewo, kudutsa mmisewu yowopsya ndi kuwoloka pa misewu yaikuluikulu iyi, mmene ngozi ndi zinthu. Chikhulupiriro chanu mwa Mulungu chimakuwongolerani inu kuti muzidutsa, mwanjira yina, chimakubweretsani inu kuno ndipo chimakutengeraninso pobwerera. Ndife okondwa kwambiri kukhala ndi abwenzi a mtundu umenewo. Ine ndikupempherera madalitso olemera a Mulungu pa inu.

9 Tsopano, Lamlungu lathali, ine—ine ndinati, "Chabwino, ife tidzayankhula, ndiyeno ine ndidzangoitanitsa mzere wa pemphero." Ine ndakhala ndikuyesetsa kuti ndikonze njira inayake, kuyesetsa kuti ndipeze njira yoti ndizipempherera anthu ochulukirapo. Ndipo ngati ine ndingamawadutsitse ochuluka kwambiri monga Lamlungu lapitali, ine. . . winawake adzakhala akundipempherera ine. Ine ndinachoka kuno, pafupifupi thuu koloko. Ndipo ine—ine sindinapereke makadi a pemphero.

10 Kupereka makadi a pemphero ndi ntchito yovuta. Ine sindikudziwa ngati inu mumadziwa zimenezo, kapena ayi, anthu amakuda iwe. Ndipo M'bale Banks Wood, ananena, tsiku lina, pamene ife tinali uko ku Kentucky, kuti adzadzipereka ndipo adzakhala akupereka makadi a pemphero ngati Billy akanati asabwere. Chotero Billy, pokhala mwana wanga yemwe, inu mukudziwa, chifukwa, iwo. . . Ine ndimalandira makalata angapo, "Iye anandilonjeza ine khadi la pemphero ndipo iye sanandipatse ine ilo. Kumupachika pang'ono!" Chotero iwo. . . Iye sangakwanitse kuwapereka iwo kwa aliyense. Ndipo ife sitingakwanitse kumawatengera ochuluka pa mzere! Mukuona? Iye amayenera kuti azinditeteza ine.

11 Ndipo—ndipo pamene ife timachoka, mpongozi wanga wamkazi anati, "Bill, ukuyenera kumubwezeretsanso Billy abwerere mmenemo ndi makadi a pemphero, kapena," anati, "iwe sulimba nthawi yaitali."

12 Ndipo, chotero, koma pamene ine ndinadzalakwitsa, panali poyamba kuzindikira zamumtima, ndiye winawake anadzabwera, nkudzati, "Ndinaiwala, amayi amafuna kuti apemphereredwe." Inu mukudziwa chimene iwo akubwerera, ndi chifukwa cha kuzindikira zamumtima kumeneko, inu mwaona. Chotero, koma, sindikuwaimba iwo mlandu. Inenso ndikhoza kuchita chinthu chomwecho. Mukuona? Ine ndingachite. . . Ndife anthu, ndipo ife tonse timafuna

kukhala moyo, ndipo timafuna kuti tizidziwa zoti tizichita. Ndicho chimene ife tiri. . .Koma iwe ukhoza kungofika penapake ndi zinthu zimenezo, iweyo, za mphatso, ndipo kenako iwe umangokhala ngati wosulukiratu, pamene izo zichitika kangapo.

13 Ndipo chotero M'bale Banks akanati apereke makadi apemphero mmawa uno, ndipo zinachitika kuti Billy anabwera usiku watha. Chotero ine ndinaganiza kuti izo zingakhale zoyipa, kumutenga mwamuna wa mbiri yabwino, zinthu monga M'bale Wood, kuti azikapereka makadi apemphero, kuti anthu azimufinya iye. Ine ndikuganiza kuti Billy samakhala nazo vuto. Iye wakhala nazo izo pa iye nthawi yaitali, chotero iye amangozisiya izo zizichitika. Chabwino.

14 Tsopano—tsopano sabata ikubwerayi ine ndidzakhala ndiri ku Dallas, Lachisanu likubwerali usiku, pa msonkhano waukulu wa Voice of Healing. Ngati kuli anthu aliwonse kozungulira kumeneko, ine ndikuyenera kukakhala kumeneko usiku umodziwo, kuti ndidzakayankhule mu msonkhano wawo waukulu. Ndipo ine ndikufuna kuti ndidzakayankhule pa phunziro la *Mafikiridwe Aku Chiyanjano*, Ambuye akalola.

15 Ndipo kenako, mwina, mwinamwake Lamlungu likubwerali, limenelo lidzakhala Lamlungu lotsatira likubwerali, ngati Ambuye alola. Tsopano sindiri wotsimikiza kwambiri. Ngati Ambuye alola, ine ndikufuna ndidzabwererenso ndi kudzayankhula pa phunziro limene ine ndimayenera kuyankhulapo lero, *Mphepo Mu Kamvuluvulu*. Ndipo ine ndimati ndipempherere odwala, lero. Ndipo zimenezo ziri ngati kudzudzula kwakuthwa kwa—kwa mpingo chifukwa cha machimo ake. Ndipo—ndipo limenelo si phunziro labwino kwambiri kuyankhulapo pomwe iwe uti uyitanitse mzere wa pemphero. Iwe uyenera kumanga chikhulupiriro cha anthu ku a. . .ku pemphero, ndi kwa Mulungu, ndi kukhala ndi chikhulupiriro. Chotero ine ndinamuuza M'bale Neville kuti alengeze kuti ine ndidzakhala ndikuyankhula mmawa uno pa phunziro lina, kumanga chikhulupiriro mwa anthu, kwa Mulungu. Mawu ena, kuwadzudzula anthu chifukwa—chifukwa chosasunga malamulo a Mulungu. Mwanjira iyi, ndi kuwamangiriza anthuwo, kuti akhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Inu mukuona?

16 Ndipo kuseri mchipinda chopempherera mmawa uno, kapena mchipinda chojambulira kumbuyo uko, mzanga wakale wamng'ono wa ine, M'bale Kidd, eyite-chakuti, wausinkhu wa zaka eyite, wakhala pano. Ambiri a inu mukukumbukira pamene ine ndinathamangira kwa iye mmawa wina, iye anali—iye anali pafupifupi. . .zinachitika pafupifupi chaka chapitacho, kuyandikira kumeneko tsopano. Akufa, akudwala moyipitsitsa, ndipo madokotala anamupatsa iye sabata yokhala moyo. Kapena, osati sabata, iwo. . .Sakanakhala

moyo kufikira mmawa woti adzamubweretse iye kuno, pafupifupi mmawa utatu zisanachitike. Ndipo tsopano iye anali atatsika kufika mpaka handiredi ndi faivi, kapena chinachake chonga chomwecho. Iye anati, mphindi pang'ono zapitazo, iye wabwerera ku handiredi ndi sarte-thuu. Anati iye akumverera ngati mnyamata.

17 M'bale Kidd, ine ndikudabwa ngati inu mungathe kungoimirira, kuti anthu akadziwe yemwe mlaliki wakale uyu ali. Ndi uyo pamenepo. Tiyeni tinene kuti, "Zikomo Ambuye." [Osonkhana akuti, "Zikomo Ambuye!"—Mkonzi]. Bambo kufa ndi khansa, mu chimenecho—mu chikhalidwe chimenecho. Iye ali ndi bwenzi lokondeka pamenepo. Ine ndingakonde iye ataimirira, nayenso. Ine basi. . .Mlongo Kidd, bwanji inu mutaimirira pamenepo? Tsopano, iye. . .Mukuona momwe iye wadzukira mwachangu? Mwabwino kuposa momwe ine ndingathere. Mulungu amdalitse M'bale ndi Mlongo Kidd. Madalitso olemera a Mulungu atakhala pa. . .Zikomo inu, mlongo.

18 Iwo amavutika kudutsa mmapiri a Kentucky, kukwera-ndi-kutsika mtinjira ta mmunda wa malasha, kuthamangitsidwa kunja, kutulutsidwa panja, ndi kusekedwa, kuzunzidwa, kumakhala moyo pakudya chirichonse chimene iwo angathe. Kumagaya chimanga chimene iwo angachipeze panjira, penapake, ndi kumakhalira moyo Ufumu wa Mulungu. Ndipo usinkhu wa zaka eyite zakubadwa, akulalikira Uthenga, apobe. Tsopano, iwo akalamba kwambiri kuti azipita kumeneko, chotero ine ndimapempherera nsalu za pemphero ndipo ndimazitumiza izo kwa iwo, ndipo iwo basi—amangopitirira kumazitengera izo ku zipatala ndi zinthu monga choncho. Anthu amabwera ndi kumadzatenga zimenezo. Tsopano, zimenezo zafika kwenikweni mu mtima. Sichoncho izo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ngati inu simungathe kupita kunja kukakumana nawo, inu mutha kuwatumizira nsalu ya pempherero, monga chomwecho, anthu kumakhala ndi chikhulupiriro. Ndizo zabwino kwambiri.

19 M'bale Rogers muno, nayenso, penapake muno lero, apongozi ake aamuna a M'bale Creech, mzanga wa ine wokondedwa kwambiri. Ndimapita ku nyumba kwake monga momwe ine ndimapitira kwa Charlie ndi Nellie ndi iwo kumusi uko tsopano, ndi kumusi ku Kentucky. Ndipo—ndipo ndinkakonda kupita kumeneko ndi kukasaka, nthawi zonse, ndi iye. Ndipo kuno, osati kale kwambiri, pafupifupi miyezi sartini yapitayo, dokotala anamutsegula iye. "Ndi khansa, ndipo," anati, "iye wapita."

20 Ndipo ine ndinaganiza, "Mzanga wakale wofunika!" Msirikali wakale, Nkhondo Yoyamba Yapadziko lonse, mwamuna wochirimika kwenikweni, banja lake. Ndipo ine ndinamubatiza iye mu Dzina la Yesu Khristu, zaka zambiri

zapitazo, ku chikhululukiro cha tchimo lake, ndikudziwa nthawi imeneyo kuti iye anayikidwa mu Thupi la Khristu, ndipo anali wokonzeka kuti apite kukakomana ndi Mulungu. Ine ndinaganiza, "M'bale wanga wofunika ayenera kuti atsogole tsopano." Izo zinali atangotha masomphenya amenewo, kapena masomphenya amenewo asanabwere kwa ine, a Kumwamba. Ndipo kenako ine ndinapita kumeneko kuti ndikamuwone iye, ndipo mchipindamo munadzabwera utawaleza. Mulungu anasintha zinthu. Zimenezo zakhala miyezi sartini yapitayo, ndipo iye akadali panobe lero, akumadya.

21 Iye anamwa mtundu wina, akumwa mtundu wina wa mapirisi a salfa, anamuwotcha iye pakhosi pake *apa*. Ndipo iye akhala mu mzere wa pemphero, ine ndikuganiza, mmawa uno, abwera. Ndipo ine ndikudziwa kuti ine ndalengeza izo Billy atapereka kale, kapena apereka, ndimadziwa kuti iwo apereka makadi a pemphero. Ine ndinamuuza mpongozi wake wamwamuna, mzanga wabwino, M'bale Creech, kuti amubweretse—amubweretse iye. Ndipo ine ndinaganiza, ngati ine ndamuphonya iye, ndiye ine ndikanamugwira iye ndi kumuyika iye mu chimodzi cha zipinda zopempherera izi kuno. Koma iye anali ndi khadi la pemphero. Ndipo ine ndinati, "Busty, ndikufuna kuti upite kunja uko." Dzina lake ndi Everett. Ife timangomutcha iye Busty, mwachidule. Ndipo iye—iye. . .Ine ndinamuuza iye, "Tuluka ndipo ukalowe mu mzere wa pemphero. Ine kulibwino ndikupempherere iwe pamene kudzoza kukadalipo, kwa zimenezo." Chotero ine ndimakonda kukhala. . .Ngati ndikudziwa kuti ine ndikhala ndikupemphereredwa, ine ndimafuna kuti winawake akhale wodzozedwa pamene iye akundipempherera ine.

22 Tsopano tiyeni titembenuzire mu Baibulo lathu, mmawa uno, titsegule ku Bukhu la Rute. Ine ndiwerenga Lemba lina kuchokera mu izi, kuchokera mu Bukhu la Rute. Ndipo tsopano basi ife tisanafikire phunziro ili. . .Ngati ine ndingathe, ine ndikufuna kuti ndilengeze mutu wanga wa mmawa uno, ndi wotchedwa: *Muwomboli Wachibale*. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwufikire iwo kuchokera kumbali zinayi zosiyana, pa chiwombolo.

23 Ndikuganiza, Lamlungu lathali, ndimalalikira za momwe Khristu anadzera kudzatiwombola ife. Ndiyeno, lero, ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa: Kodi Muwomboli ndi chiyani? Kodi Iye amakhala bwanji Muwomboli? Ndipo, mukumbukire, Muwomboli amakuwombolani inu kwathunthu, pamene Iye akukuwombolani inu; kuchokera ku machimo anu, kuchokera ku matenda anu, kuchokera ku chirichonse chimene chiri cholakwika. Iye ndi Muwomboli.

24 Tsopano, ife tisanafikire iwo, tiyeni tiweramitse mitu yathu ndi kuyankhula kwa Iye, kudzera mu pemphero. Ndipo tsopano ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikudabwa kuti ndi

angati mmawa uno, mu Kukhalapo, amene angafune kuti akumbukiridwe mu pemphero, pokweza manja anu mmwamba ndi kumati, "Mulungu, onani...inu mukulidziwa pempho langa"? Mulungu akudalitseni inu, aliyense.

25 Atate Athu Akumwamba, ndine wokondwa kwambiri, lero, kuti ilipo Mphamvu Yapamwamba yopambana, podziwa kuti, Mulungu, kuti ife tikhoza kukufikirani kudzera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu, ndi kukhala ndi—yankho ku zimene ife tafunsa. Monga mu msonkhano wapitawo, ife timayankhula za momwe anthu ankayendayenda mu zikopa za nkhosa ndi zikopa za mbuzi, ndipo anali osowa pokhala, akufunafuna Mzinda umene wowumanga ndi wowupanga wake anali Mulungu. Akudziwa kuti ngati akanati adzafikire kwa Iye kamodzi, ngati iwo angapeze kumene Iye anali! Monga Yobu, wakale, anati, "Ngati ndingakhoze kupita, kukagogoda pa chitseko Chake," mwanjira yina. "Ngati ndingakhoze kukapeza kumene Iye—Iye amakhalako, ine ndikanapita Kwathu ndi Iye, ndipo ndikana—ndikanakayankhulana naye Iye, maso ndi maso." Koma panalibe njira yoti munthu angachite zimenezo, chifukwa iye anali atachimwa, ndipo anali atadzilekanitsa yekha ndipo anasanduka mlendo kwa Mulungu.

26 Koma kudzera mwa Mmodzi wofunikayo Amene anabwera ndipo anadzatsegula njira, ndipo anakhulululukira machimo athu, ndi kutibweretsa ife pamaso pa Mulungu, osati ngati alendo, koma ngati ana akubwera kwa Atate wawo. Podziwa kuti Iye adzatipatsa ife chosowa chirichonse chimene ife tipempha. Lamulo limodzi lokha linalembedwa, ndiro, "Ngati inu mungakhulupirire." Umenewo ndi mgwirizano. Satana amadzinenera kuti ife sitidzakhulupirira, ndipo Mulungu amati ife tidzakhulupirira. Tsopano nkhondo ili mkati, ndipo chigamulo ndi chathu kuti tipange. Mulimonse momwe chigamulo chathu chingapangidwire, ndi momwenso izo zidzakhalire. Ndipo izo nzolembedwa modabwitsa kwambiri, "Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira."

27 Ndipo ife tikukhulupirira, lero, tikubwera, tikufikira kwa Inu chifukwa cha kukonderedwa Kwauzimu, kukupemphani kuti Inu mumve zopempha zathu. Ndipo dzanja lirilonse limene linakwezedwa mmwamba, Inu mukudziwa pansi pa dzanja limenelo, mu mtima mwawo, chimene chimatanthauzidwa. Pakuti kunalembedwa, kuti, "Inu mumadziwa zolinga ndi maganizo a mmalingaliro, ndipo mukhoza kuzindikira malingaliro." Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu muyankhe molingana ndi chuma Chanu ndi chisomo Chanu, kwa chopempha chirichonse chimene chatchulidwa.

28 Ife tingapemphenso lero, Ambuye, kuti Inu mundithandize ine, wosowekera kwambiriyo, mwinamwake, mwa omvetsera; podziwa kuti, patsogolo panga apa, pali ogulidwa a Magazi a Ambuye Yesu. Ndi amenewo, mwinamwake, ochimwa akhala

pano, amene ali omangidwa kwambiri ndi tchimo, kuti zingakhale zovuta kwa iwo, zosatheka, pafupifupi, kuti iwo afikire ku malo woti angamulandire Khristu, malingana ngati Satana wawamangitsitsa iwo mu mphamvu yake. Koma podziwa kuti kunalembedwa, "Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda."

29 Ndipo mutipatse ife mphamvu lero, Ambuye, kudzera mu kulalikira kwa Mawu, kuti ikatulutse mdierekezi aliyense wa kukaikira ndi matsenga ndi mantha, kuchokera mmitima ya anthu ndi malingaliro. Kuti iwo amene ali omangidwa ndi zokhumudwitsa ndi kukaikira athe kubweretsedwa mmikono ya Khristu. Ndipo kunalembedwanso, kuti, "Iwo adzayika manja awo pa odwala ndipo iwo adzachiritsidwa." Alipo iwo pano amene ali Akhristu, ndipo ndi omangidwa ndi ziwanda za matenda.

30 Ambuye, ndipatseni ine mphamvu lero, ya Mzimu Woyera, kuti ndikawombole munthu wodwala aliyense ndi wosautsika amene ali pano mchipindachi lero, kuti Mzimu Woyera wawukulu uthe kukhala ndi mauyambiriro mu mtima uliwonse ndi aliyense amene ali mu Kukhalapo Kwauzimu.

Muyankhule kwa ife kudzera mu Mawu Anu. Mawu Anu ndi Choonadi. Sindikudziwa basi choti ndinene, koma tikuyembekezera pa utsogoleri wa Mzimu Woyera, kuti Iye atitsogolere ife ndi kutilondolera ife mu Choonadi chonse. Mupereke izi, Ambuye. Mudzitengere ulemelero kwa Inumwini. Ndipo mumudzoze mtumiki Wanu. Ndipo Mawu Anu anadzozedwa kale. Ife tikupatsani Inu matamando, pamene Inu mukuzitengera izo ku mtima uliwonse, monga ife tiri ndi chosowa. Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikupempha izi, Mwana wa Mulungu. Ameni.

31 Tisanawerenge, ine ndikhoza kunena mbalume yaying'ono iyi imene ndimaikonda kwambiri:

> Ngati muli ndi mitsinje imene simungathe kuwoloka,
> Ndipo muli ndi mapiri amene simungathe kudutsapo,
> Mungokumbukira, Mulungu Kumwamba ndi katswiri mu zinthu zimene ena sangathe kuzichita.

32 Ine ndikuwerenga kuchokera mu Bukhu la Rute, mutu wa 1.

> *Tsopano kunali mmasiku amene oweruza ankalamulira, munali njala mdzikomo. Ndipo munthu wina wa ku Betelehemu-yuda anapita kukayenda mdziko la Moabu, iye, ndi mkazi wake, ndi ana ake aamuna awiri.*
>
> *Ndipo dzina la mwamunayo linali Elimeleki, ndipo…mkazi wake Naomi,…dzina la ake…*

*ana aamuna anali Maloni ndi Kiliyoni, aku Efurata waku Betelehemu-yuda. Ndipo analowa mdziko la Moabu, ndipo anakhala kumeneko.*

*Ndipo Elimeleki, mwamuna wa Naomi anamwalira;. . .iye anatsala, ndi ana ake aamuna awiri.*

*Ndipo anadzitengera akazi mwa akazi a ku Moabu; dzina la. . .mmodzi anali Olipa, . . .dzina la winayo Rute: ndipo iwo anakhala kumeneko pafupifupi zaka teni.*

*. . .Maloni ndi Kiliyoni anamwaliranso awiri onse; ndipo* akaziwo *anasiyidwa. . .mzimayiyo anasiyiridwa ana ake aamuna awiri ndi mwamuna wake.*

Ndipo *iye ananyamuka ndi apongozi ake, kuti abwerere kuchoka mdziko la Moabu: pakuti iye. . . anamva mu. . .*iye anamva *kuti* A*MBUYE* *anachezera anthu ake powapatsa iwo mkate.*

*Chomwecho iye anaturuka ku malo amene anali, ndi* apongozi ake aakazi *awiri pamodzi naye; ndipo anapita paulendo wawo kubwerera ku dziko la Yuda.*

*Ndipo Naomi anati kwa* apongozi *ake awiri, Pitani, bwererani aliyense ku nyumba ya amake:* ndipo *AMBUYE akuchitireni inu zokoma, monga inu munachitira ndi akufa, ndi ine.*

Ndipo *AMBUYE apereke* kwa *inu kuti mupeze mpumulo, aliyense wa inu mu nyumba ya mwamuna wake. Kenako iwe anawapsyopsyona iwo; ndipo iwo anakweza* mawu *awo, ndipo analira.*

*Ndipo iwo anati kwa iye, Ndithudi ife tibwerera ndi inu kwa anthu a mtundu wanu.*

*Ndipo Naomi anati, Bwereraninso, ana anga aakazi:* inu *mupita nane bwanji? kodi mudakali ana aamuna ena mmimba mwanga, kuti* inu *mukhale. . .amene. . . angadzakhale* amuna *anu*?

*Bwereraninso, ana anga aakazi, pitani njira yanu; pakuti ine ndakalamba kwambiri kuti ndingakhale* ndi *mwamuna. Ngati ine ndingati, ndiri ndi chiyembekezo, ngati ine ndingakhale* ndi *mwamuna usiku uno, ndi kuberekanso ana aamuna;*

*Kodi inu mungadikirire* mpaka *iwo* atakhala *aakulu? kodi* inu *mungadzakhale chifukwa cha iwo. . .*kwa zawo*. . .osakhala ndi amuna? ayi, ana anga aakazi; pakuti zikundiwawa kwambiri* chifukwa *cha inu kuti dzanja la AMBUYE lachoka monditsutsa ine.*

*Ndipo iwo anakweza* mawu *awo, ndipo analiranso: ndipo Olipa anawapsyopsyona apongozi ake; koma Rute anakakamira kwa iwo.*

*Ndipo iye anati, Taonani, mlamu wako wabwerera kwa anthu ake, ndi* kwa mulungu *wake: bwerera iwe umutsatire mlamu wako.*

*Ndipo Rute anati, Musandiumirize kuti ndikusiyeni inu,* kapena *kuti ndibwerere osakutsatani inu: pakuti* kumene *inu mupita, ine ndipita; ndipo kumene inu mukagona, inenso ndikagona: anthu anu adzakhala anthu anga,. . .Mulungu wanu* adzakhala *Mulungu wanga:*

*Kumene inu* mudzafera, *ine ndidzaferako, ndipo kumeneko ine ndidzaikidwa:* AMBUYE *andichitire ine chomwecho, ndipo awonjezerenso, ngati kanthu koma imfa ilekanitse* ine ndi. . .*inu ndi ine.*

33 Ine ndikufuna kupereka mutu nkhani yaying'ono iyi mmawa uno, pamene ndikuphunzitsa izo, kuyesetsa kuti ndibweretse chikhulupiriro kwa inu, cha chiwombolo, ndi chimene icho chiri, ndi momwe mungachilandirire icho. Ine ndikufuna kuitcha iyo: *Muwomboli Wachibale.*

34 Tsopano, *kuwombola* chirichonse, ndi "kuchibwezeretsanso icho." Chinachake chimene chinatayika, ngati kuchiyika mu shopu ya pinyolo. Ndipo inu mumapita ndi kukachiwombola icho, icho chimawomboledwa ndi mtengo. Kenako chimadzakhala katundu wanu, mutatha kuchiwombola icho. Koma lamulo la chiwombolo, mu Israeli, ankayenera kukhala wachibale, kuti akawombole katundu kapena chinachake chimene chinatayika.

35 Nkhani yathu ikuyambira mu nthawi ya olamulira a ku Israeli, omwe anali oweruza, Yoswa atafa. Ndipo kuti mupeze chithunzi chokongola kwambiri cha ichi, muwerenge pafupifupi mitu faivi kapena sikisi yoyambirira ya Samueli Woyamba, ndipo inu mu—inu muimvetsa nkhani yeniyeni ya izo.

36 Koma ife tilumphirapo tsopano kuti tipeze nkhani yayikulu kuchokera mu izi. Chimene, nthawi yina yapitayo, ine ndinayambapo pa Bukhu ili la Rute, ndipo ndinakhalapo kwa masabata atatu kapena anayi, ndikudutsa mu ilo. Ndinayambira pa Bukhu la Chivumbulutso, kamodzi, ndipo zinatenga chaka chonse, pafupifupi, kuti ndilidutse Ilo. Basi Lemba laling'ono lirilonse limagwirizana lina ndi limzake, kwathunthu, kudutsa mu Baibulo. Izo ndi zokongola. Chotero, timadziwa kuti Baibulo ndi lodzozedwa. Pakuti, mwamasamu ndi njira iliyonse, palibe mabukhu ena olembedwa omwe samadzitsutsa okha penapake.

37 Bukhu ili linalembedwa pafupifupi zaka foro sauzande motalikana, Mabukhu a m'Baibulo. Ndipo iwo analembedwa ndi ena. . .Ine ndaiwala basi kuti ndi amuna angati omwe

analemba iwo. Ndinadzakumbukira. Koma, pepani. Ine ndikufuna kuti ndinene sikisite chakuti, koma ine—ndine—ndine. . .ine ndikhoza kulakwitsa pamenepo. [M'bale akuti, "Forte."—Mkonzi]. Forte. Amuna forte analemba Baibulo, mu danga la zaka masauzande motalikana, osamadziwana wina ndi mzake, kapena kumawonana wina ndi mzake, kapena kumawerenga pambuyo pa mzake, nthawi zambiri. Ndipo palibe mawu amodzi amatsutsana ndi ena. Iwo ndi odzozedwa!

38 Tsopano, anthu ambiri amayang'ana pa Bukhu ili la Rute, monga iwo amanenera, "Ndi nkhani ya chikondi ya m'Baibulo." Baibulo ndi nkhani ya chikondi. Baibulo lonse ndi nkhani ya chikondi.

39 Sikuti Ilo ndi nkhani yachikondi yokha, koma Ilo ndi mneneri. Sikuti Ilo ndi kokha mneneri, koma Ilo ndi mbiriyakalenso. Osati kokha Ilo ndi a—nkhani ya chikondi, mbiriyakale, mneneri, Ilo ndi Mulungu Mwiniwake. Chifukwa, "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu." Chotero, Mawu ndi Mulungu atasindikizidwa. Izo zikuyenera kukhazikitsa izo, m'bale; Mulungu atasindikizidwa. Yehova, atasindikizidwa pa Bukhu. Ndipo palibe chirichonse cha izo basi mtundu wina wa nthano yopeka chabe, koma izo zonse ndi Choonadi mwamtheradi. Gawo lirilonse la Ilo, muyikepo moyo wanu. Ilo liri Pamenepo. Ilo ndi Choonadi, ndipo Mulungu adzaikira kumbuyo Mawu Ake.

40 Ndipo nkhani iyi inalembedwa, ndi mipukutu yonse yakale. Pamene iwo ankaligawa Baibulo, amuna oyera, pamene iwo ankayesera kuti ayike izo pamodzi mu Chipangano Chakale, Bukhu ili la Rute linali limodzi mwa Mabuku odziwika amene iwo anawavomereza. Chifukwa chiyani? Ngati iyo ili chabe nkhani ya chikondi, nchifukwa chiyani olemba ndi anzeru akale anavomereza Bukhu ili ngati lodzozedwa? Chifukwa, muli vumbulutso lobisika mwa Ilo. Ndipo mu vumbulutso lobisika ili, inu mumagwiramo tanthauzo lenileni. Ilo lidzakufikitsani inu pafupi kwenikweni kwa Mulungu.

41 Ndipo ine ndikupemphera, moyo wanga wonse, mmawa uno, kuti Mulungu agwire mtima uliwonse, ukhale kakasi kwambiri, mpaka Iye adziulule Yekha, basi chimene Iye ali, mu nkhani iyi; chimene Iye ali kwa inu; momwe mungamulandirire Iye. Ndipo pamene inu muchiwona icho kamodzi, chimakhala chophweka kwambiri, mumadabwa momwe inu munkachiphonyera icho. Koma icho chikhoza kuwululidwa kokha ndi Mzimu Woyera.

42 Tsopano, ambiri, powerenga Baibulo, amaliwerenga Ilo, amangoimirira ndi kuwerenga tsamba, ndi kuwerenga tsamba. Inu simudzalimvetsa konse Ilo. Chifukwa, Ilo liri mu mikuluwiko. Ndipo Yesu anamuthokoza Mulungu polipanga Ilo monga chomwecho. Anati, "Inu mwazibisa Izo kwa maso a

anzeru ndi aluntha, ndipo mwaziulula Izo kwa makanda amene angaphunzire."

43 Monga ndimanenera kawirikawiri. Akazi a Branham akhala kumbuyo uko, mmawa uno. Koma ndikakhala kutsidya kwa nyanja, iye amandilembera ine kalata. Iye amati, "Wokondedwa Bill, ine ndakhala pano, usikuuno, ndi ana. Ine ndikuganiza za iwe." Ndipo iye amapitirira ndi kulemba zimene angalembe. Koma ine—ine ndimamukonda iye, ndipo ndimamudziwa iye bwino kwambiri, ine ndimatha kumawerenga pakati pa mizere. Ine ndimadziwa ndendende chimene iye akunena, mwaona, kaya walemba izo apa kapena ayi. Mukuona? Chifukwa, ndimadziwa chimene iye akunena. Nchifukwa chiyani zimakhala chomwecho? Kumeneko ndi kulumikizana kwapafupi. Ndife amodzi. Mukuona? Ndipo iye amadziwa chikhalidwe changa, ine ndimadziwa chake. Iye sama . . .

44 Iye akhoza kungokhala ndipo nkumandiyang'ana ine. Ine ndikhoza kukuuzani inu chimene iye ati anene, mwaona, chifukwa ine—ine ndimamudziwa iye bwino chomwecho. Ndipo iye akhoza kuchita nane mwanjira yomweyo. Tsopano, chimene chimachita izo, ndi kudalirana wina ndi mzake. Chikondi!

45 Dzulo mmawa, tinali titagona pabedi mochedwerapo pang'ono, ndipo ana samayenera kuti apite ku sukulu, ndipo ife tinayamba kuyankhula za zinthu zosiyanasiyana. Ndipo momwe . . . "Kodi chidani ndi chiyani?"

46 Ine ndinati, "Chidani chinali ndi chiyambi, chotero icho chikuyenera kukhala ndi mathero. Chikondi chinalibe chiyambi, chotero icho chiribe mathero. Chidani ndi kwanthawizonse. Chikondi ndi Muyaya. Chidani chimayamba ndipo chidani chidzatha. Chikondi sichinachite kuyamba nkomwe ndipo Icho sichidzatha nkomwe." Mukuona? Icho chinali Chamuyaya.

47 Ndipo pamene mwamuna amukonda mkazi ndi kumukwatira iye chifukwa ndi wokongola chabe, padzakhala mathero a zimenezo. Koma pamene mwamuna amupeza mkazi amene amamukonda, iye samachidziwa chifukwa chake, koma amangomukonda iye. Ndipo mkaziyo nkupeza mwamuna amene akumukonda, ziribe kanthu mawonekedwe a iye. Iye amangomukonda mkaziyo. Iye amamukonda mwamunayo. Ameneyo ndi mzake Wamuyaya mu Ulemelero. Iwo adza- . . . Imfa kapena chinthu chirichonse sichingawalekanitse iwo, chifukwa iwo ndi ochokera ku Muyaya. Ndipo iwo anatulukira, mu danga la nthawi, ndipo adzabwereranso ku Muyaya. Muyaya watsika pansi mu thupi, lotchedwa nthawi, kenako lidzabwereranso mmwamba kupita ku Muyaya kachiwiri. Ilo silingawonongeke.

48 Mkazi amene ali wokongola, kukongola kumeneko kudzazimirira, motsimikiza basi. Muzipatse izo zaka zingapo. Mwinamwake, lero, iye akuzipotokola pa msewu, mkazi wina

wamng'ono wovala mwatheka, akutumiza miyoyo yambiri ku gehena kuposa mabara onse mdziko. Koma iye amadzipotokola yekha mumsewu, kumaganiza kuti iye ndi chinachake. Monga Baibulo linanenera, "Iwo akanadzakweza makosi, mwadama, *akudzigwedeza*," (izo zikutanthauza kuzipotokola) "pamene iwo akupita," mtsiku lotsiriza. Akukwaniritsa Malemba, ndipo osadziwa izo. Iwo amaima pabwalo, atavala zovala zamakhalidwe oyipa, amuna akumamuyang'ana iye, ndipo osadziwa. Iye akhoza kukhala waukoma, kwa mwamuna wake kapena bwenzi lake lalimuna, monga iye angakhalire; koma, pa Tsiku la Chiweruzo, iye adzayankha chifukwa chochita chigololo ndi mahandirede a amuna. Mzimu uli pa iwo, ndipo iwo sakudziwa izo. Baibulo linati, "Amaliseche, akhungu, ndipo osadziwa izo." Gawo lomvetsa chisoni ndi lakuti, "Osadziwa izo."

49 Koma kodi inu mukudziwa, thupi lopangidwa bwino laling'ono limenelo, limene Mulungu wamupatsa mtsikana ameneyo, likhoza kudzakhala litavunda podzafika nthawi ino Lamlungu likubwerali? Mwamuna wamtali, wakuda ndi wokongola ameneyo akhoza osakhalanso kanthu koma basi mulu wa zinyalala, podzafika Lamlungu likubwerali. Izo zonse zimawononongeka.

Koma icho cha mkatimo, Mulungu, chikondi, amakhala kwa Muyaya. Chotero, muziyang'ana cha mkaticho. Maso anu akhale pa cholingacho.

50 Tsopano, nkhani iyi ikuyambitsa chinachake mwanjira imeneyo, ngati mkazi wokondedwa, wokoma. Dzina lake anali Naomi. *Naomi* amatanthauza "chokondweretsa." *Elimeleki* anali mwamuna wake, amatanthauza "kupembedza." "Kupembedza kokondweretsa" kunali banja lake. Iwo anali ndi mwana wamwamuna, *Maloni,* mmodzi amene amatanthauza "matenda." Ndipo *Kiliyoni*, winayo, amatanthauza "wotopa, wolunda, wachisoni." Ndi limenelo banjalo.

51 Ndipo munadza njala mdziko la Israeli. Ndipo kulakwitsa koyamba kumene Myuda amapanga konse, ndi, kulisiya dziko limenelo. Mulungu anawapatsa iwo dziko limenero. Pamene Abrahamu anapatsidwa dzikolo, Mulungu anamuuza iye kuti asadzachoke mdziko limenero. Ndipo iye analakwitsa pamene anatsikira kumeneko mu Gerari, anakalowa mu vuto. Myuda samayenera kuchoka ku Palestina. Amenewo ndi malo ake oyikidwako.

52 Ndipo iwo athamangitsidwa, padziko lonse lapansi. Ndipo tsopano iwo akubwereranso. Oh, ndi nkhani yokongola kwambiri imene ife tiri nayo pano, mmawa uno. Iwo akubwerera.

53 Naomi anakakamizika kutuluka chifukwa cha njala, Naomi ndi Elimeleki, ndipo iwo anapita ku Moabu.

54 Tsopano kuti mumvetse kumbuyo kwa nkhaniyo, kuti, pamene mukumvetsera, muthe kumvetsa chimene iyo ili.

Tsopano, Moabu-. . .Amoabu anachokera kwa mwana wapathengo, amene anali ana aakazi a Loti. Atathawa moto wa Sodomu, mwa chisomo cha Mulungu, kenako ana aakazi anawaledzeretsa abambo awo ndipo anagona ndi iye, ngati mkazi. Iwo anabereka mwana. Ndipo mmodzi wa iwo anayambitsa, ndipo anabweretsa a—fuko la Moabu, kuganiziridwa kuti anali Akhristu, koma anali osakanizika mu chikunja. Ndipo, mwaona, kulisiya dziko lolonjezedwa, ziribe kanthu kuti zinaipa bwanji, kukakhala mlendo mdziko lina, zimabweretsa mavuto.

55 Ndipo nthawi iliyonse imene wokhulupirira achoka pa malo ake opatsidwa ndi Mulungu! Nthawi zambiri, mu ndale, chisankho ichi chimene chikubwerachi ndi zina zotero, munthu wabwino akhoza kukhala munthu wabwino, ndipo iye amachoka pa malo amenewo. Monga mtumiki wina amene ine ndikumudziwa, anapikisana nawo kuti akhale meya wa mzinda. Ndipo pamene iye anatero, anachoka pa malo ake otumikira, ndipo Satana anamugwira iye.

56 Ngati Mkhristu aliyense achoka pa malo amenewo. "Chabwino, ine ndingopita kumeneko, usikuuno, ndikakhala ndi anyamata mu bala, kwa kanthawi. Ine sindikachita choyipa chirichonse. Ine ndikangomwa chakumwa pang'ono." Inu mwachoka pa malo anu. Bwererani. Inu mukungokhazikitsa njira yanu ya mavuto.

57 "Oh, atsikana ena onse amasuta. Ine ndikangoyesera imodzi." Inu mwachoka pa malo anu. Musachite zimenezo. Mungokhala mmaiko-akwanu. Musatero, "Chabwino, aliyense pano, iwo amanditchula ine, 'Wachikulire kwambiri.' Iwo amanditchula ine, 'Wachikale.'" Mukhalebe pamenepo, mulimonse. Amenewo ndi malo anu. Mukhalebe mwa Khristu.

58 Naomi, chifukwa cha njalayo, anayendayenda kuchoka mdzikolo ndipo anapita ku Moabu, akufunafuna mkate. Iye sankayenera kuti achite zimenezo, chifukwa ena onsewo anatsalira mu Yudeya, Betelehemu. Betelehemu amatanthauza, *Betele,* "nyumba ya Mulungu," nyumba ya matamando. Ndipo iwo amakhala kumeneko.

59 Ndipo iye anachoka ndi mwamuna wake. Ndipo ana ake aamuna awiri anakwatira atsikana a Chimoabu. Koma ngati Mulungu anadzozeratu chinachake kuti chidzachitidwe, icho chidzachitika mulimonse. Icho ndi chifukwa chake ine mwamtheradi ndimakhulupirira mu kukonzedweratu, kudziwiratu kwa Mulungu kwa zinthu.

60 Kenako ife tikupeza, cha kumeneko, imfa inakantha banjalo, ndipo iwo anayamba kubwerera. Kupha. . .Mnyamatayo anamwalira, anyamata awiri onse anamwalira, ndipo abambowo

anamwalira. Ndipo Rute anayamba kubwerera, Olipa, ndi Naomi.

61 Tsopano, ine ndikufuna kuti ndifanizire, mmawa uno, Naomi, dona wamkulu, kwa mpingo wa Orthodox, mpingo wa Chiyuda wa Orthodox. Rute, Mmoabu, wa Amitundu, kukhala Mpingo wa Chikhristu, Mpingo Watsopano.

62 Ndipo ine ndikufuna kuti ndizifikire zimenezo, kuchokera mu magawo foro osiyanasiyana, Rute. Ine ndazilemba izo apa. Rute, akusankha, akupanga chisankho chake; Rute, akutumikira; Rute, akupuma; Rute, akulandira mphotho. Pamene ife tikubwerera: Rute, akupanga chisankho; Rute, atapanga chisankho chake, kenako Rute akutumikira; kenako Rute akupuma; kenako Rute akulandira mphotho.

63 Tsopano, ali panjira akubwerera, inadzafika nthawi, monga iye pokhala choyimira cha Mpingo, kapena Mkhristu. Monga, munthu aliyense payekha amaimira fuko lonse la Chikhristu. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Inu, mu khalidwe lanu, momwe inu mumachitira ndi zomwe mumachita, inu mumaimira Thupi lonse la Khristu. Inu mumati, "Koma ndine membala wamba chabe." Izo ziribe kanthu. Pamene inu mutenga dzina limenelo la Mkhristu, inu mumaimira Khristu ndi Mpingo Wake. Inu mudzikhala monga chomwecho. Inu mudzikhala monga njonda, monga madona. Musamachite konse zinthu za dziko lapansi, chifukwa maso onse a Kumwamba ndi a dziko lapansi akuyang'ana pa inu, kuti muyimire chinthu chimodzi chimenecho. Ziribe kanthu kuti ndinu ofooka chotani, kuti ndinu aang'ono chotani, chilimikani, chifukwa ndinu Mkhristu.

64 Tsopano, Rute anali wachikunja, ankatumikira fano, ndipo chomwechonso Olipa. Ndipo iwo anali panjira yawo, akubwerera ndi apongozi aakazi. Chifukwa, iye anamva, kuti, uko mu Betelehemu-Yudeya, kuti Mulungu anali atachotsa mliriwo, ndipo anthu anali ndi mkate. Iye anali atakhala kumeneko pafupifupi zaka teni, chotero Edersheim amati, "pafupifupi zaka teni," wa zambiriyakale.

65 Ndipo akubwerera, wachisoni (ndipo mwamuna wake atafa, ana ake atafa), ali ndi azipongozi ake aakazi awiri. Kenako iye anadzatembenuka, ankayenera, ndipo anawayang'ana iwo, ndipo anati, "Inu mupita nane chifukwa chiyani? Tsopano, palibe chimene mungachite koma mavuto basi." Anati, "Pepani kuti dzanja la Mulungu latambasula monditsutsa ine."

66 Ndi kangati kamene Israeli anaganizapo zimenezo, osadziwa kuti linali dongosolo la Mulungu! Momwe khoma lolirira liri kunja kwa Yerusalemu, likadali kumeneko! Miyala yakale ya kachisiyo, iwo ankaitola iyo ndipo anamangira khoma. Ndipo iyo imakhulidwa, yosalala, chifukwa cha misozi ndi kulira, kwa manja Achiyuda, kulira ndi kumamupempha Yehova, "Yehova!" Iwo sakuzindikira kuti ora lawo layandikira tsopano.

Makoma olirira, “Miyala imeneyi nthawiyina munkakhalamo Likasa la Pangano. Mfumu Davide ankayang’ana pa miyala imeneyi. O Yehova, muli kuti Inu?” Mukuona? Osadziwa kuti posachedwapa Mfumu yake idzabwereranso, Muwomboli wake. Iwo ankayenera kuti aponyedwe kunja, kwa kanyengo pang’ono.

67 Naomi anadabwa, “Nchifukwa chiyani nkono wa Ambuye wandichitira ine nkhanza, azipongozi anga aakazi? Mulungu wandiponyera ine kunja. Ndine wotayika. Sindikudziwa chimene ine ndinachitapo, koma ndine wotayidwa.” Mukuona?

68 Mulungu amapanga programu Yake. Chifukwa, “Zinthu zonse zimachitira ubwino kwa iwo amene amamukonda Mulungu,” ziribe kanthu chomwe izo ziri.

69 Iye anati, “Inu mubwerere kwa amayi anu, ndipo mukapeze mpumulo m’nyumba ya amayi anu. Amuna anu afa. Ndipo ndinu achichepere, akazi okongola. Bwererani. Bwererani kumene munachokera. Kumeneko mukapeza mpumulo. Mulungu akuchitireni inu chifundo, chifukwa inu munali achifundo kwa akufa. Ndipo mwakhala moyo waukoma kuyambira pomwe amuna anu anamwalira. Ndipo inu mwakhala achifundo kwa ine, mkazi wamasiye wachikulire wopanda mwamuna, ndipo inu munamamatira kwa ine. Bwererani, ndipo Mulungu akupatseni inu mpumulo m’nyumba mwanu.” Iwo analira.

70 Iye anati, “Ngati. . .Ndine wokalamba. Ine sindingakhalenso ndi ana ena. Koma ngati ine nditati ndikhale ndi mwamuna ndipo nkukhala ndi mwana, izo zidzapanga ubwino wanji? Inu simungamuyembekezere mwana ameneyo.” Ilo linali kwenikweni lamulo mu masiku amenewo. Kuti ngati mchimwene afa, kapena. . .ndipo, wake, mchimwene winayo pokhala wosakwatira, iye ankayenera kumutenga mkazi wake kuti adzutse dzina kwa mchimwene wake wakufayo. “Koma, iye,” anati, “inu simungamuyembekezere iye, makanda awa. Chotero, bwererani ndipo mukadzipezere nokha mpumulo m’nyumba za amuna anu. Bwererani kwa amayi anu.”

71 Ndipo, Olipa, woyimira mpingo wofunda umene unayambapo, woyimira mpingo umene sudzapita njira yonse. Iye anati, “Izo zikumveka zabwino kwambiri.” Chotero, iye anawapsyopsyona apongozi ake ndipo anabwereranso. Ndicho choyimira wokhulupirira wofunda, amene adzakhulupirire kuti Yesu ndi Khristu, kenako nkutembenuka ndipo nkubwerera mu chinthu chimene iye anatulukamocho. Kwa munthu amene ati adzagwire njira ndi onyozeka apang’ono a Ambuye, ndipo kenako nkutembenuka, nkubwerera mmbuyo. “Monga galu ku masanzi ake, ndi nkhumba ku matope ake,” monga Baibulo linanenera.

72 Tsopano, iye anabwerera kwa milungu yake. Nthawi zambiri ife timabwerera kwa milungu yathu—ya chiyambi chathu. Mwinamwake ife timaika maso achisiliro pa chinthu

cholakwika. Ife tidzabwereranso ku kusilira. Mwinamwake ife tiri ndi mafano akumwa, mafano osuta, mafano abodza, mafano akuba, mitundu yonse ya mafano; ndipo kenako nkuvomereza ndi kudzabatizidwa, ndipo kenako nkupotolokanso. Ndi chinthu chomvetsa chisoni bwanji! Kumbukirani, ilo silinadzanenenso dzina lake. Iye anachotsedwa chifukwa cha chisankho chake.

73 Mpingo wofunda, wokhulupirira wofunda, monga wokhulupirira aliyense amayimira mpingo. Wachimerica aliyense amaimira America. Wachigerman aliyense amaimira Germany. Mkhristu aliyense amayimira Khristu.

74 Apa iye anapotoloza nsana wake, kuti abwerere ku chinthu chimene iye anatulukamocho. Momwe kuti amuna, ngakhale alaliki, nthawizina, amatenga njira ya Ambuye, ndipo pamene uyankhula kwa iwo za ubatizo wa Mzimu Woyera: "Zamkutu," amachoka kwa Iwo. Ameneyo ndi Olipa.

75 Ukawauza iwo za Dzina la Yesu Khristu, kuti, "Palibe Dzina lina pansi pa Kumwamba loperekedwa pakati pa anthu limene inu mukuyenera kupulumutsidwa nalo. Chirichonse chimene inu muchita mmawu ndi mu ntchito, muchite zonsezo mu Dzina la Yesu Khristu, ngati palibe Dzina lina pansi pa Kumwamba limene inu mukuyenera kupulumutsidwa nalo." Kenako Petro anati, pa tsiku, Tsiku la Pentekoste, "Ngati inu mukufuna kuti mupulumutsidwe, mulape ndipo mubatizidwe, mu Dzina la Yesu Khristu, ku chikhululukiro cha machimo anu." Umo ndi momwe iwo amachotsedwera. Ndipo munthu, chifukwa cha kutchuka, iye amalephera kugwira Baibulo pa izo. Koma chifukwa cha kutchuka, adzapsyopsyona Mpingo, kupsyopsyona Uthenga, kumupsyopsyona Khristu, "nkutsanzika," ndipo nkubwerera kumene iye anakumbidwako. Olipa, wofunda, wochotsedwa.

76 Koma, oh, momwe ine ndimamukondera Rute wamng'onoyo! Iye ankayenera kupanga chisankho. Ine ndinkayenera kupanga chisankho. Inu mukuyenera kupanga chisankho. Inu simutuluka konse pa zitseko izi, mmawa uno, popanda mtundu wina wa kusankha. Inu simuchoka mchipinda chino, lero, kaya ndinu mwamuna kapena mkazi wabwinoko, kapena mwamuna woyipitsitsa kapena mkazi. Kukana Iwo, inu mudzakhala woyipitsitsa. Zidzakhala zokuvutani nthawi yina, kuti inu mudzafike kwa Iwo. Kapena, mutuluka muli wabwinoko.

77 Chinabwera chiwonetsero mmoyo wake. Pamabwera chiwonetsero mmoyo wa aliyense. Ndipo Rute ankayenera kupanga chisankho. Chotero, Baibulo linanena kuti apongozi ake anamuuza iye, "Ubwerere kwa milungu yako monga wachitira mchemwali wako. Ubwerere monga wofundayo wachitira. Kodi bwanji iwe osabwerera mmbuyo."

78 Mlaliki wa Uthenga, "Ngati inu mukufuna kupita, kazipitani." Mlaliki weniweni woona amene adzaziyike zimenezo pamaso pa gulu la anthu, "Inu mupange chisankho

chanu. Inu muyime pa mapazi anu." Wofunda, wosakhazikika, wolowa-ndi-kutuluka, sanganene zimenezo. Koma mtumiki weniweni wa Mulungu amayika izo pa chilolo chanu, "Mupange chisankho chanu."

79 Rute anati, "Ine ndidzapita kumene inu mukupita. Anthu anu adzakhala anthu anga. Mulungu wanu adzakhala Mulungu wanga. Kumene inu mukakhala, ine ndikakhalako. Kumene inu mudzafere, ine ndidzaferako. Ndipo kumene inu mudzayikidwe, ine ndidzayikidwako." Ndi chimenecho chisankho chenicheni.

80 "Ambuye, ine ndikutengani Inu ngati Mpulumutsi wanga. Ngati Baibulo likuti, 'Lapani ndipo mubatizidwe, Dzina la Yesu Khristu,' zimenezo ine ndizichita. Ngati Baibulo linati ine 'ndikuyenera kulandira Mzimu Woyera,' chimenecho ine ndidzachita. Ngati Baibulo limandiuza ine, 'Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,' zimenezo ine ndizikhulupirira. Ine ndidzatenga Baibulo ndi Mulungu, pa chimene Iye analemba ndi chimene Iye ali, ziribe kanthu zomwe wina aliyense wanena." Ndi ameneyo Rute weniweni.

81 Iye anapanga chisankho chake. Iye ankayenera kuti mwina abwerere mmbuyo kapena apite patsogolo. Ife tayima pa malo omwewo, mmawa uno, kubwerera mmbuyo kapena kupita patsogolo. Musabwerere konse mmbuyo. Tiyeni tidzipita patsogolo.

82 Kupitirira mpaka ku dziko lolonjezedwa iwo anapita, kupita ku dziko la anthu achirendo. Rute, woyimira wa wokhulupirira tsopano. Chiyani? Kodi wokhulupirira ndi chiyani? Pamene iye kapena iye atuluka, munthu wochokera ku za mdziko, iye amabwera mwa Achikhristu okhulupirira. Akazi amene ankasuta, kumwa, ndi kusewera makadi ku mabungwe, ndi zina zotero, ndi kukhala ndi mitundu yonse ya zinthu zapamwamba, ndipo ngati mtundu wina wa "mbalame yonyowa," koma tsopano iye wasintha. Iye wapanga chisankho choyenda ndi Mulungu. Tsopano iye akumabwera mwa anthu omwe samakhulupirira zinthu za mtundu umenewo. Iye ndi mlendo. Iye akuyenera kuti aziyenda ngati mwendamnjira. Iye sakuidziwa miyambo yawo. Iyo yonse ndi yachirendo, kwa iye. Iwo sakudziwa choti achite. Izi ndi zimene Rute ankayenera kuti achite. Ndi zomwe mukuyenera kuti muzichita. Ndi zomwe ndikuyenera kuti ndizichita.

83 Pamene ine ndinamuvomera Khristu, ine ndinathamangitsidwa kwathu komwe. Pamene ndinamulandira Khristu, abwenzi anga aamuna, abwenzi aakazi, aliyense, anandiponyera ine pansi. Ndinapita uko ndi gulu la anthu akale amene anali ndi Mzimu Woyera ndipo ankakhulupirira mwa Mulungu, nkumamutumikira Iye. Atsikana, anali kumusi uko mu mpingo umenewo, anali osiyana ndi atsikana omwe ine ndinkayenda nawo. Iwo ankawoneka mosiyana. Iwo ankachita

mosiyana. Anali achilendo, ndipo ndinkawawopa iwo. Iwo anali anthu osiyana.

84 Icho ndi chimene Rute ankayenera kuti achichite. Iye ankayenera kuti abwere kuchokera kwa ake omwe, kupita kwa anthu ena. Iye anatembenuka mtima. Iye anapanga chisankho.

Ndipo inu mupange chisankho. Inu mukuyenera kupanga kusankha kwanu. Inu mukufuna kuti mubwerere ku zinthu za mdziko, kapena inu mukufuna kumapitirira ndi Mulungu?

85 Kodi inu mukufuna kuti muzichita ngati dziko ndi ena onse? Kenako nkumupsyopsyona Khristu "ndapita" ndi kubwerera mmbuyo.

Koma ngati mukufuna kutenga njira yanu ndi onyozeka apang'ono a Ambuye, gwiritsitsani ku dzanja losasintha la Mulungu. Mosalabadira zomwe dziko lonse likunena, inu mugwiritsitse pamenepo. "Mulungu ananena chomwecho. Zimenezo ndi zoona. Ine ndikuzikhulupirira Izo, ngakhale ine sindingakhoze kuziwonetsera izo mmoyo mwanga. Mulungu ananena chomwecho. Ine ndikukhulupirira Izo. Ine ndikugwira pomwepa."

86 Umo ndi mmene iye anachitira kwa Naomi. "Ine sindikusiyani inu. Ine ndipita kumene inu mukupita. Anthu anu adzakhala anga. Momwe iwo amachitira, umo ndi momwe ine ndikachitire. Momwe iwo amapangira, ndi momwe ine ndizipangira. Zomwe iwo amadya, ndi zomwe ine ndizikadya. Kumene inu mudzafere, ine ndidzakaferako. Kumene inu mudzaikidwe, ine ndidzakaikidwako. Ndipo Ambuye achite zambiri kwa ine ngati ndilephera kulikonse." Chimenecho ndi chisankho chachindunji chenicheni. Mulungu akufuna zisankho zachindunji kuchokera mu Mpingo Wake.

87 "Chabwino, Ambuye, ngati Inu mutangoti mundidalitse ine ndipo nkundichitira ine *ichi*, ine ndidzachita *chakuti-ndi-chakuti*." Chimenecho si chisankho.

88 "Mulungu, ine sindikusamala zimene inu muti muchite ndi ine, ine ndidzapita mulimonse. Ngati ine ndifa, chabwino. Kukhala moyo kapena kufa, chirichonsecho! Ngati iwo andiseka ine, kundisereula ine, sizipanga kusiyana kulikonse, ine ndidzapita mulimonse." Chimenecho ndi chisankho chachindunji, chonga chimene Rebekah anapanga asanamuone nkomwe Isaki.

89 Makolo ake anati, "Muloleni mtsikanayo ayankhe. Mtsikanayo, ndi wausinkhu, muloleni iye ayankhe."

90 Iye anati, "Ine ndipita." Chisankho chachindunji, chopangidwa mwachangu. Iye anakakamira kwa icho. Icho ndi chimene Rute anachita. Olipa anabwerera mmbuyo.

91 Iwo anapitirira pa ulendowo. Rute, mu mtima mwake, asakudziwa kumene iye ankapita, koma choyimira cha Mpingo.

Ife tikuyenda, monga Abrahamu. Amwendamnjira mdziko lachilendo, pakati pa anthu achilendo.

Ndipo iye anapita, ndipo potsiriza iye anafika mchipinda ndi malo amene Naomi ankamubweretsa iye. Ndipo kodi iye anapeza chiyani? Aliyense akumusisita iye kunsana kwake ndi kumati, "Rute, ndife okondwa kuti iwe wabwera kuno"? Iye anapeza kusagwirizana. Iye anapeza chinachake choyipa. Iye anapeza vuto.

92 Ndipo alaliki amene angakuuzeni inu kuti, "A—moyo Wachikhristu ndi kama wa maluwa ophweka," iye mwina akukunamizani inu kapena iye sanavomereze chomuchitikiracho iyemwini. Dziko limadana nawe iwe. Ndipo anthu adzakuda iwe. Iwe ukuyenera kutenga njira ya onyozeka apang'ono a Ambuye, ndi kumasekedwa, kusereulidwa, kapena china chirichonse. Iwe ukuyenera kukhala wosiyana. Iwe wabadwira ku Fuko lina.

93 Mkazi wanga . . . Monga ine ndi—ndibwereza izo kenanso; zikuwoneka bwino kwambiri kuchita izo. Anandifunsa ine, "Kodi ndi chifukwa chiyani akazi Achikristu samavala zovala zimenezo monga momwe akazi ena amachitira?" Ine ndinati . . . Ndinati, "Ndife tonse Achimereka, sichoncho ife?"

94 Ine ndinati, "Ayi, bwana."

95 "Chabwino, ife ndi chiyani?"

96 Ine ndinati, "Ife si Achigerman, Achifaransa, Belguims, Swiss, Achiafrica, kapena Achimerica, kapena palibe aliyense wa iwo."

97 "Koma ife ndi chiyani?"

98 Ine ndinati, "Ndife Akhristu." Wachimerica amachita monga Wachimerica, Wachigerman amachita monga Wachigerman, chifukwa umenewo ndi mzimu wa fuko lawo. Ndipo ife tiri ndi Mzimu wa fuko. Umenewo ndi Mzimu Woyera wochokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba, ndipo inu mumachita monga Iwo. Umakupangitsani inu kumachita monga iwo amachitira Kumeneko, chifukwa ndinu a Dziko lina.

99 Ife timakhala ku America, zimenezo ndi zoona. Limenelo ndi gawo la thupi. Koma moyo umene umatitsogolera ife, khalidwe lathu, ndi wochokera Kumwamba. Ife timakhala moyo wochokera Kumwamba chifukwa tinabadwa kuchokera Kumwamba. Akhristu onse amachokera Kumwamba. Yesu anati, "Ine siwochokera kuno. Ndine wochokera Kumwamba. Ngati ndikanakhala wochokera kuno, nzika Zanga zikanandimenyera Ine nkhondo. Koma Ufumu Wanga ndi Wakumwamba." Chomwechonso munthu aliyense amene wabadwira mu Ufumu wa Mulungu, iye ndi wochokera Kumwamba.

100 Tsopano, tikupenya tsopano. Pamene tikupitirira, tikuwapeza iwo akufika mu kukhumudwa. Kodi uko ndi kumene inu munapitako, pamene inu munalandira Mzimu Woyera? Ndithudi munatero. Ine ndinatero. Kusereulidwa, ndi chirichonse.

101 Ndiye, zindikirani, moyo unali wovuta kwa iye. Ndipo iwo umakhala wovuta ukakhala Mkhristu. Chifukwa iwe umayenera kudzisintha wekha kuchoka ku moyo umodzi, wa chisangalalo ndi zosangalatsa za dziko lapansi, kupita ku moyo wina, wodzipereka kwa Mulungu. Inu mukuyenera kudzisinthanso nokha, kupita ku mbali *iyi*.

102 Ndipo Rute ankayenera kudzisintha kuchoka ku kukhala mdziko la chakudya chambiri, ndi chirichonse cholemekezeka, kupita kwa anthu amene ankaseka, kumusereula iye, kupita mdziko limene iye ankakunkha mmunda chimene iye ankadya. Kuyika izo pa mpango wake ndi kupita nazo kunyumba. Ndipo ankasinja izo ndi kupanga mkate, ndipo iye ndi apongozi ake aakazi ankadya iwo.

103 Pamene iye anali kumeneko, iwo anadzapeza, pamene iye ankakunkha, kapena akupita kuti akakunkhe. . .Tsopano, iye anapanga chisankho chake. Kumeneko kunali kusankha kwake.

104 Tsopano, chinthu chotsatira chimene iye akuyenera kuchita ndi kutumikira.

105 Ndipo ndicho chimene Mpingo ukuyenera kuchita. Mpingo, mutatha kupanga chisankho chanu, mukuyenera kuti mutumikire. Mumutumikire Mulungu molingana ndi chithunzi Chake, molingana ndi dongosolo Lake. Inu muyenera kumutumikira Mulungu.

106 Rute, akupanga chisankho. Tsopano, Rute, akutumikira pansi pa chisankho chake. Tsopano penyani miniti yokha. Tsopano iye akupita kumunda, akukakunkha.

107 Tsopano, amayi ake anamuuza iye; chimene chiri, Chipangano Chakale chikuuza Chatsopano, inu mukudziwa. Amayi ake anamuuza iye, anati, "Ife tiri ndi wachibale, ndipo dzina lake ndi Boazi. Iye ndi munthu wolemera. Ndipo iye ndi wachibale wapafupi. Iwe upite kumunda wake. Ndipo mwinamwake. . .Iwe usapite kumunda wina; upite kumunda wake."

108 Momwe Mzimu Woyera umatiuzira ife kuti tisalowe mu mtundu wina wa a—bukhu la mpingo, mtundu wina wa katekisimu, koma kupita ku Munda wa Mulungu, Chipangano Chakale, Baibulo. Musanene kuti, "Chabwino, ife tikanena *ichi*. Ndipo ife tikanena *ichi* kwa pemphero. Ife tikakhala ndi *ichi*." Mukhale pomwepo ndi Mundawo. Mulowe Mmenemo, chifukwa Iye ndi Wachibale wapafupi.

109 Mawu a Mulungu, Chipangano Chakale, ndi Wachibale wapafupi kwa Chatsopano. Mpingo Wakale ndi mayi wa Mpingo Watsopano, mwaona, Mkhristu, wokhulupirira. "Usapite kumunda wina. Ukakhale mmunda mwake momwe. Ndipo mwinamwake, tsiku lina, iwe ukhoza kudzapeza chisomo ndi iye."

110 Ndipo tsiku lina, pamene iye anali mmunda, mnyamata wolemera uyu, dzina lake Boazi, wolamulira, mwamuna wachuma, anabwera, ndipo anamuwona iye. Oh, pamene iye anamuwona iye, iye anagwa naye mchikondi. Iye anamuganizira kuti iye anali mkazi wodabwitsa. Iye analikonda khalidwe lake. Inu mukukumbukira, iye anati, "Ine ndikudziwa, ndiye anthu akudziwa, kuti ndiwe mkazi waukoma." Anapanga chisankho chake, choyera komanso chomveka. Anabwereranso, anakhala ndendende basi momwe iye ananenera kuti adzachitira.

111 Mwinamwake, lero, iwo amati, "Tikudziwa kuti iwe ndi Mkhristu. Ife tikudziwa kuti iwe ndi munthu wa Mulungu, chifukwa palibe munthu angachite zozizwitsa izi pokhapokha Mulungu atakhala ndi iye."

112 Ndicho chimene Nikodemo ananena kwa Yesu, anati, "Rabbi, tikudziwa kuti ndinu mphunzitsi wochokera kwa Mulungu. Palibe munthu angachite zinthu zimene inu mukuchitazi pokhapokha Mulungu atakhala ndi iye." Pamene, iye ankatha kumuwona Iye atakhala pamenepo ndi kuzindikira malingaliro omwe amu mtima mwawo.

113 Mkazi anakhudza chovala Chake. Anatembenuka, anati, "Ndani wandikhudza ine?" Onse a iwo anakana izo. Anayang'ana mmbuyo mwa omvetsera ndipo anati, "Iwe, wa vuto la magazi pamenepo, chikhulupiriro chako chakuchiza iwe."

114 Anati, "Palibe munthu angachite zimenezo pokhapokha Mulungu atakhala naye. Ife tikudziwa kuti Inu munachokera kwa Mulungu. Ife sitingakulandireni Inu, chifukwa ife tidzathamangitsidwa mu mpingo." Mukuona?

Mpesa womezanitsidwa umenewo, M'bale West, monga ife timayankhulira usiku watha, iwo adzakuthamangitsirani inu panja. "Koma, pansi mu mtima mwathu, ife tikudziwa kuti inu munachokera ku Mpesa wapachiyambi." Khristu ndi Mpesa; ndife nthambi. "Ife tikudziwa, chifukwa ife tikuwona Moyo womwe womwewo umene uli mwa Mulungu, uli mwa Inu."

115 Ndicho chimene Boazi anachiwona mwa Rute, chisankho chachindunji chija, mkazi wa ukoma uyo atayima pamenepo. Ndipo iye anagwa naye mchikondi.

116 Tsopano, ine ndikufuna inu muzindikire. Naomi, mpingo wakale, anayamba kufotokoza kwa Rute malamulo onse okhudza chipembedzo chake, monga Chipangano Chakale ndi

mthunzi wa Chatsopano. Tsopano, ine ndikufuna inu mumvetse nkhani iyi pomwe apa.

117 Tsopano, ndikufuna kuti ndiwonetsere mithunziyo. Chipangano Chakale chimafotokoza Chatsopano, ngati inu muti mungochiwerenga Icho, pakuti Icho ndi mthunzi wotsogolera wa Chatsopano. Tsopano, ngati ine ndikanati ndimapita cha ku khoma ilo, ndipo ine sindinadziwonepo ndekha nkomwe, ndipo ine ndikuwona mthunzi wanga, ine ndingadziwe, nkukhala ndi lingaliro la momwe ndingawonekere. Ndipo ngati inu simu (inuyo) kudziwa chimene Chipangano Chatsopano chiri, muwerenge Chakale ndipo inu mudzawona mthunzi wake. Mukuona? Ndiyeno pamene Chipangano Chatsopano chizibwera, inu muziti, "Bwanji, ndithudi, ichi ndi Chimenecho." Bukhu la Ahebri, kubwerera mmbuyo, Paulo akufotokoza izo.

118 Tsopano, zindikirani mwatcheru tsopano. Pamene Rute anati, kapena . . . Naomi anati kwa Rute, anati, "Tsopano, iye ndi wachibale wathu. Ndipo ngati iwe ungapeze chisomo ndi iye, iwe udzapeza mpumulo." Oh, mai! "Ngati ungapeze chisomo, iwe udzapeza mpumulo." Boazi ankaimira Khristu, Mwamuna wolemera, wolowa wa zinthu zonse, Ambuye wa zokolola. Oh, mai! Motani, pamene Boazi anabwera atakwera kunja uko, mu chokwera chimenecho, akuyang'ana pozungulira mmindayo, ndipo maso ake anagwera pa Rute! Iye anali bwana. Iye anali mbuye wa zokolola. Ndipo iye anapeza chisomo pamaso pake.

119 Icho ndi chimene Mpingo ukuchita, lero. Pamene Ambuye wa zokolola akudutsa, Iye sakuyang'ana nyumba yaikulu, nsanja zazikulu, makwaya-ophunzitsidwa bwino. Iye akufunafuna aliyense payekha payekha, amuna ndi akazi amene ali odzipereka ndipo anapanga chindunji kwa Khristu, anadzipatulira okha ku utumiki Wake. "Mulungu, ine ndikuwakhulupirira Iwo, Mawu aliwonse a Iwo. Pamene Mawu Anu anena chirichonse, ine ndimakhalabe ndi Iwo. Amenewo ndi Mawu Anu. Ine ndimawakhulupirira Iwo, Mawu aliwonse." Icho ndi chimene Iye akuchifuna; Ambuye wa zokolola. Ndicho chimene Iye akufuna kupereka, Mzimu Woyera, kwa iwo amene ali ndi njala ndi ludzu. "Odala ndi inu akumva njala ndi ludzu, chifukwa mudzakhuta." Iye akuyesetsa kuti awupeze Mpingo umenewo, lero.

120 Tsopano, kenako, Rute anapemphedwa kuti achite chinachake chimene chinali chochititsa manyazi, koma iye anali wololera chifukwa anali atapanga chisankho chake. Ndi choyimira bwanji cha wokhulupirira! Ndi choyimira changwiro bwanji!

121 Naomi, mpingo wakale, anati, "Pita kumusiko, usikuuno. Ndi nyengo ya bare." Oh, ndi ganizo lokongola bwanji lomwe ife tingakhale nalo pamenepo!

122 Naomi ndi Rute anabwera basi mu nyengo ya bare. Nyengo ya bare inali nyengo ya mkate, nyengo imene mkate watsopano unkaperekedwa. Ndipo Mpingo, mmasiku otsiriza ano, utadutsa zaka thuu sauzande za ziphunzitso zachikunja ndi zinthu, wabwera mu nyengo ya bare, ndi chiwisi cha Moyo, Mkate watsopano, uchi wochokera Kumwamba. (Russell, kukamba za mkate wa chikhungwa cha uchi!) Ndi Umenewutu, Mkate Wochokera Kumwamba. "Ine ndi Mkate wa Moyo. Makolo anu ankadya manna, ndipo anamwalira. Koma Ine ndi Mkate wa Moyo umene umachokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba. Ngati munthu adya Mkate uwu iye sadzafa konse." Ndipo Mpingo mmasiku otsiriza ano kuno, ukubweretsedwamo, pakali pano, mu nyengo ya bare.

123 Rute, Wamitundu, wochotsedwa, wothamangitsidwa, wabweretsedwa mkati, kuti adzavomerezedwe ngati Mkwatibwi. Khristu anabwera, mu nyengo ya bare.

124 Iye anati, "Tsopano uvale zovala zako." (Osati, "Uvule zovala zako.") Ndi zotsutsana bwanji ndi lero! "Udziveke zovala zako, pamene ukupita kukakomana naye iye. Iye akupita kuti akapete bare, usikuuno. Upite kumeneko ndipo uvale zovala zako. Ukadziphimbe wekha, kuti ukakomane naye iye."

125 Lero, iwo akufuna kuti azidzivula okha. Ukadziphimbe wekha. "Upite kumeneko, chifukwa iye akupeta bare. Ndipo ukatero ukayike chizindiro malo amene iye akagoneko." Kodi inu munachita zimenezo? Pa Gologota. Zaka zambiri zapitazo, ine ndinalemba mu mtima mwanga pamene Iye anataya moyo Wake, kuti Iye akhoze kunditenga ine. Ukayike chizindikiro pamalo amene iye akagonepo. Ukapenyetsetse pamene Iye anagona. Ndicho chimene wokhulupirira aliyense akuyenera kuchita. Uzikumbukira zimene Iye anakuchitira iwe. Uthenga wa Lamlungu lapitali, pa *Ulendo Wopita Ku Kalvare*, muzikumbukira zimene Iye anakuchitirani inu.

126 Iye anati, "Ukaike chizindikiro pamene iye akagone. Kenako iye akakagona, kuti apumule, iwe udzapite kukagona pa mapazi ake." Osati kumutu kwake; mapazi ake, wosayenera. "Ndipo ukatenge bulangete limene iye walifunda, ndipo ukalikokere ilo pa iwe." Oh! Inu mukuziona zimenezo? Oh, mai! Ine ndikudziwa kuti inu mutha kumaganiza kuti ndine wotentheka. Koma zimenezo zikungondikwanira ine molondola basi, Mzimu wa Mulungu umenewo. Muike chizindikiro pamene Iye anagona, Kalvare; mmene Iye anagona mmanda; mu Getsemani. Muike chizindikiro, ndipo mukwawire ku mapazi Ake. Mukagone pansi pamenepo ndi kufa, inumwini, kwa chanu. . .Ndi zimenezotu. Mukadziphimbepo nokha, pamwamba, ndi siketi Yake. Iye anati, "Siketi," iye anaitcha iyo.

127 Ndipo Rute anati, "Zimene inu mwanena, zimenezo ine ndikachita."

128 Oh, ndi chisankho chachindunji bwanji kwa wokhulupirira! "Zimene Baibulo limanena, zimenezo ine ndikachita. Limati, 'Lapani ndipo mubatizidwe, Dzina la Yesu Khristu,' ine ndikachita zimenezo. Ngati Ilo likuti, 'Pitani ku dziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga,' ine ndikachita zimenezo. Ngati Ilo likuti, chirichonse chimene Ilo likunena, 'Yesu Khristu yemweyo dzulo, kwanthawizonse.' Chimene Ilo likunena kuti ine ndichite, ine ndikachita chimenecho." Mukuona, Mpingo ukutenga malamulo Ake kuchokera mu Mawu. Iye anakagona pansi.

129 Tsopano, kumbukirani, icho chinali chamanyazi kwa mkazi wamasiye wamng'ono ameneyo kuti akagone pambali pa mwamuna uyu, pa mapazi ake. Chochititsa manyazi, kwa dziko lakunja.

130 Oh, kodi inu mungapirire izo? Ndi izi apa. Penyani. Penyani. Ndi chimenechitu. Mpingo, mtsikana, mnyamata, wamkulu kapena wamng'ono, akufunsidwa kuti adzipatule okha kuchoka kwa dziko lapansi, ndi kubwera ku malo, Ufumu wa Mzimu Woyera, ndicho chamanyazi kwa dziko lapansi. Mmitima mwawo iwo akudziwa chimene chonsecho chiri. Koma, kwa dziko, iwo amadzakhala otentheka. Iwo amadzakhala oyera odzigudubuza kapena chinachake pa lingaliro limenero, dzina lina lamanyazi. Koma Mpingo ukufunsidwa kuti uchite zimenezo. Kodi inu mukulolera kuti muike chizindikiro malowo, ndi kugona pansipo, kulolera kuti dziko likutchuleni inu chirichonse chimene iwo akufuna?

131 Nyimbo yakale, tinkakonda kuyimba:

> Ine ndayamba kuyenda ndi Yesu yekha,
> (Mukuona?)
> Ndiri ndi mtsamiro, ngati Yakobo, mwala;
> Ndipo ndidzayenda njira ndi onyozeka ochepa
> a Ambuye,
> Ine ndayamba ndi Yesu. Ine ndikupyolatu.

132 Ndi zimenezotu. Ziribe kanthu, ine ndidzalipira mtengo wake chirichonse ena angachite. Ngati zikutanthauza kuchititsidwa manyazi, ngati zikutanthauza kutaya nyumba, kutaya—kutaya banja, oyanjana nawo anu onse, abwenzi aakazi, abwenzi aamuna, chirichonse chimene chikutanthauza, ine ndipita ndekha. Ine nditenga njira. Ngati woyandikana naye wanga anena kuti ndine "woyera wodzigudubuza, wa chipentekoste, kapena wotentheka," ine sindikusamala chimene iwo anganene. Sizipanga kusiyana mpang'ono pomwe kwa ine. Ine ndayamba. Ine ndapanga chisankho changa momveka bwino, ndipo ine ndikupyola.

133 Tsopano, iye anali mmodzi yekhayo amene akanakhoza kumupatsa iye mpumulo, kuchokera ku minda yotopetsa imeneyo ya kukunkha. Oh, izo zinali zokoma kwambiri

pamene, Boazi, pamene iye anamupeza iye kunja mmunda. Ine sindingaphonye izi. Boazi anamupeza iye ali kunja mmunda. Iye anati, "Taona." Iye anati, "Kodi iwe ndi ndani?"

Anati, "Dzina langa ndine Rute."

"Oh, wachi Moabu amene wabwera kudzakhala nafe."

"Inde."

134 "Ine ndamva za iwe. Iwe usamapite kuminda ina." Ah! Ine ndikuzikonda zimenezo. "Usayambe kuthamangathamanga. Khala pomwe pano mmunda mwanga. Ukhale ndi waine." Iye anamukonda iye. "Ukhale pano. Ukhale ndi ine. Usapite kumathamanga uku ndi uku. Ukhale pano."

135 Ngati inu mumawukhulupirira Uthenga, khalanibe ndi Iwo. Mukuona? Ziribe kanthu chomwe mtengo wake uli, khalanibe ndi Iwo. Muzipitirira. "Ngati izo zikutanthauza, kupereka *ichi, icho,* kapena *chinacho*. Ndipo ine ndikuyenera kusiya kumwa kwanga, ndikuyenera kusiya kuba, kunama. Ine ndikhala pomwepo ndi Iwo." Mukuona?

136 Ndipo izo zinanenedwa kachiwiri, iye anati, "Tsopano, iwo sakuvutitsa iwe, chifukwa ndawalamulira anyamata kuti asakunyoze iwe." Ameni. Ine ndikuzikonda zimenezo, chitetezo chake. Kodi ndi ndani ananena zimenezo? Mbuye wa zokolola.

137 Mukhale osamala. "Musakhudze odzozedwa Anga. Musawachitire choipa aneneri Anga." Kodi nkulondola uko? "Pakuti indetu, ine ndinena kwa inu, zingakhale bwino kwambiri kwa inu kuti mwala wamphero ukanakolowekedwa pakhosi panu, ndi kumizidwa mnyanja, ngakhale kuti muwakhumudwitse aang'ono awa, aang'ono Anga." Nkulondola uko? "Musabweretse ngakhale chokhumudwitsa kwa iwo."

"Ine ndawalamulira iwo kuti asakugwire iwe." Oh, penyani dziko limenelo! Ndi lozunza. Iwo ali ndi ora lawo likubwera.

138 Kenako iye anapita kwa anyamatawo, enawo. Iye anati, "Tsopano, iye akukunkha kwa moyo. Tsopano, ine ndikufuna inu okolola. . .angelo inu," mwakuyankhula kwina. Icho ndi chimene iwo ali. Anati, "Ine ndikufuna angelo inu, okolola inu, kamodzi mu kanthawi, kuti muzigwetsa zodzaza mdzanja, ndi cholinga." Oh! "Musamalole kuti zonse izo zizikhala zotopetsa kwa iye. Koma kamodzi mu kanthawi, muloleni iye azimva Uthenga wabwino. Mulole mphamvu yabwino ya Mzimu Woyera izimuphimba Iye pamwamba, kamodzi mu kanthawi, kumulola Iye kuti azidziwa kuti ine ndikadali pamenepo. Muzipanga mtundu wina wa machiritso pakati pa Iye. Mudziwonetsera mtundu wina wa chizindikiro kapena chodabwitsa, kuti Iye azidziwa kuti ine ndiri pakati pa Iye." Ndi zimenezotu.

139 Kodi inu simukufuna kuti muzipeza zodzaza dzanja izo? Ine ndikuyembekeza kuti ife tipeza zina mmawa uno, sichoncho inu? Bare watsopano wodzaza dzanja. Ambuye achite chinachake

chimene Iye ankakonda kuchita. Chinachake chimene ife tikudziwa kuti Iye amachita. Iye ndi Ambuye wa Zokolola. Iye ndi Mmodzi yekhayo amene angagwetse zodzaza mdzanja. "Ine ndikulamulira Angelo kuti apite ku msonkhano umenewo mmawa uno. Ine ndikufuna kuti iwo achite chinachake, chinthu chinachake. Ine ndawalamulira Iwo, ndipo Iwo achita icho." Oh, mai.

140 Tsopano, apa, iye ankayenera kutenga gawo lamanyazi, kuti agone pansi, kutchedwa chirichonse chimene iye ankafuna kutero. Iye ankakhoza kumatchedwa hule, inu mukudziwa. Iye ankakhoza kumatchedwa mkazi wa mbiri yoipa, komabe iye sanali wotero. Ndipo anali kutsatira ndendende malamulo amene anaikidwa kwa iye. Chotero iye akupita kumusi ndipo akudziphimba yekha ndi chophimba chimene iye anali atafunda. Kodi iye anapita kuti? Kumanda. Iye anapita kuti? Kumene iye ankapumulira.

141 Pamenepo ndipamene ine ndinazipeza izo.

> Pamtanda pamene Mpulumutsi wanga anafera,
> Pamenepo apo ponditsuka ku tchimo ndinalira;
> Pamenepo ku mtima wanga Magazi anapakidwa.
>
> Pali Kasupe wodzazidwa ndi Magazi,
> Ochokera mmitsempha ya Imanueli,
> Pamene ochimwa akagwera pansi mu kusefukira,
> Amataya madontho awo onse a zolakwa.

142 Muike chizindikiro pa malo amene Iye anagonapo, ndipo mugone pamenepo ndi Iye. Kodi inu mwakonzeka kupita ku Kalvare, mmawa uno, monga ine ndinanena Lamlungu lapitali? Kodi mwawaika chizindikiro malowo mmoyo wanu? Kodi mwadzibweretsa nokha kumalo amenewo amene Yesu anapachikidwa?

143 "Oh, ife tikuyamikira zimenezo." Koma nanga bwanji za kupachikidwa kwanu? Kodi mwakonzeka kutenga njira ndi dzina lochititsa manyazilo, monga kukhala woyera-wodzigudubuza, wotentheka wachipembedzo, kapena chirichonse, chirichonse chimene mtengo wake uli?

144 Kodi mwawaika chizindikiro malowo, kuti inu mupite kumeneko ndi kukagona pansi ndi Iye, mukuti, "Ambuye, ine ndiri pano"? Ndiye chiyani? Mukokere chophimba chomwecho chimene chinali pa Iye, muchifunditse pa inu.

145 Mkazi nthawiina anati kwa Ambuye wathu, "Ambuye, mupereke kwa ana anga awiri, kuti mmodzi adzakhale kudzanja lamanja, ndi la kumanzere, mu Ufumu."

146 Iye anati, "Kodi iwe ungamwere chikho chimene Ine ndimamwera?" Ndicho chizunzo chowawa.

"Inde."

147 "Ndipo kodi iwe ungabatizidwe ndi ubatizo womwewo umene ine ndabatizidwa nawo?" Mugone pansi, mukokere chofunda chomwecho pa iye.

148 Eliya anatengedwera mmwamba. Ndipo Eliya anaponyera pansi chophimba chomwecho chimene iye anali nacho, kuti chimuphimbe Elisha ndi magawo awiri a Mzimu wake. Chinthu chomwecho, magawo awiri chabe. Mphamvu yomweyo; palibenso. Palibenso, palibe yayikulu; magawo awiri basi a Iwo.

149 Monga Mose, pamene iye anali atatopa, apongozi ake aamuna ananena kwa iye, anati, "Iwe ukudzitopetsa wekha. Pemphera kuti Mulungu awutenge Mzimu wako ndi kuwuyika Iwo pa ena." Ndipo iye anapemphera.

150 Ndipo Iye anatenga Mzimu ndi kuwuyika Iwo pa sevente ena ndipo sevente anayamba kunenera. Iwo analibe mphamvu ina iliyonse yochuluka. Iwo anali ndi makina ochuluka. Ndizo zonse. Chinthu chomwecho, anangokhala ndi makina ochuluka.

151 Umo ndi momwe izo zikukhalira, lero. Munthu mmodzi sangakhoze kuchita izo. Mulungu ali nazo zipangizo Zake zikugwira ntchito konsekonse, koma ndi mphamvu yomwe yomweyo; mphamvu yomwe yomweyo, Mzimu Woyera womwe womwewo, Yesu yemwe yemweyo.

152 Tsopano, anatenga bulangete, Mzimu Woyera, pamene iye anafa kwa iye yekha. Anaika chizindikiro pa malo amene iye anafera, pamene iye anagona kuti apumule. Kenako iye anakagona, ndipo anatenga bulangete limene linali pa iye ndipo analikokera kwa iye. Ndipo mwamunayo anadzuka, anati, "Ndi ndani ali pamenepoyo?" Iye anati. . .Iye anati, "Ine ndi Rute, wachi Moabu uja, mdzakazi wanu."

153 Ndipo iye anadzuka. Iye anati, "Ine ndikuganiza ndipo ndikudziwa kuti ndiwe mkazi wa ukoma." Ameni. Oh! Kodi izo sizikungochititsa tsemwe pang'ono mmoyo wanu? "Iwe ndiwe mkazi wa ukoma."

154 Ndipo kodi iye anayankha chiyani? "Koma iwe ndi wachibale wapafupi." Ameni. "Iwe ndi wachibale wapafupi. Iwe ukhoza kundichitira ine. Iwe ukhoza kundipumulitsa ine. Ine ndabwera kuno ndipo ndagona pano, osati ngati mkazi wamakhalidwe oipa. Ine ndagona apa, osati kuti ndidzakhale wodziwonetsera; kuti ndidzawawonetse anthu kuti ine ndikhoza kuyankhula mmalirime, kuwawonetsera anthu kuti ine ndikhoza kuvina mu Mzimu, ndi kuwawonetsera anthu kuti ine ndikhoza kufuula. Koma ndabwera kuno chifukwa iwe ndi wachibale wapafupi. Osati kudzawonetsera kuti ine ndikhoza kuchita chinachake chachikulu; koma inu

ndi abale anga. Ine ndabwera chifukwa iwe ndi wachibale wapafupi, ndipo ndiwe wekha amene ungandiwombole ine."

155 Mukuona kachitidwe ka—otembenuka mtima kwa Khristu, ku Mpingo? Mukuona? Mukuona? "Iwe ndi wachibale wanga wapafupi."

156 Ndipo iye anati, "Iwe ndi mkazi waukoma. Ndipo ine ndi wachibale wako wapafupi. Tsopano, dzifunditse wekha. Ugone pansi mpaka mmawa." Psyii! "Kungodzifunditsa mu bulangete limenero. Ndine wachibale wako. Ugone pamenepo mpaka mmawa, ukupumula." Ameni. Ameni. "Ndine wachibale wako wapafupi. Pumula!" Ameni.

157 Pamene mmawa unafika, kunja kusanache nkomwe, iye anali atasonkhanitsa mtolo wawukulu kwambiri wa bare, miyeso sikisi, ine ndikukhulupirira iyo inali, ndipo anayika iyo mu yake—shawelo yake yaying'ono ndipo anapita kwawo.

Ndipo—ndipo Naomi anati, "Mwana wanga wamkazi."

158 Inu mutadzukapo kuchoka pa guwa, ndi kubwerera mmbuyo. "Tsopano chitachitike ndi chiyani, amayi? Kodi chiti chichitikeno ndi chiyani?" Ameni.

159 "Puma." Ameni. "Puma, Rute, chifukwa mwamunayo sadzakhala ndi mpumulo kufikira atatsiriza mtengo wonse wa chiwombolo." Ameni. Ameni. Pomwepo ndi pamene ine ndaima. Ameni. Iye sadzapuma kufikira Iye atatsiriza mtengo wathunthu wa chiwombolo, kuti akuwomboleni inu, chirichonse chimene inu munayamba mwatayapo, chirichonse chimene inu munakhalapo.

160 Tsopano kumbukirani lamulo la chiwombolo, pamene ife tikuyandikira potseka, ku mapeto a msonkhano. Lamulo lonse la chiwombolo ndi ili, kuti, munthu asanawombole katundu wotayika, iye ankayenera kukhala wachibale wapafupi. Ndipo chinthu chotsatira, iye ankayenera kuti akhale munthu wolondola, munthu wolungama, kuti achite izo. Ndipo kenako iye ankayenera kukhala wa ndalama zokwanira, kuti achite izo. Ndipo kenako iye ankayenera kupanga umboni wa poyera kuti iye wachita zimenezo. Ndipo kuyambira pamenepo, uyo amakhala katundu wake.

161 Chotero tsopano yang'anani. Boazi ankaimira Khristu. Tsopano, Rute ankaimira Mpingo, inu, wokhulupirira. Ndipo tsopano, Mulungu, mu Chipangano Chakale, njira yokha imene Iye ankakhoza kubwera ndi kudzawombola chimene chinali chitatayika, Mulungu ankayenera kuti adzakhale wachibale kwa munthu. Ndipo njira yokhayo imene Mulungu akanakhoza kudzakhala wachibale kwa munthu, inali kukhala mmodzi wa iwo. Ameni.

162 Ine ndimatsutsana ndi Billy Graham, pa anthu atatu pawokha mu Umulungu, kapena mphunzitsi wina aliyense

wautatu, pa izo. Ine ndimakhulupirira mu utatu, ndithudi, koma osati mwanjira imeneyo, iwo kukhala anthu atatu. Iwo ndi Mmodzi. Nkhani ija pamenepo, payokha, inalibe china chirichonse koma icho, chikanatsimikizira izo.

163 Mulungu anadzakhala munthu. Iye ankayenera kuti adzakhale wachibale. Ndipo Iye sakanakhoza kukhala Mulungu, ndipo ife ochimwa, zolengedwa za chirengedwe Chake, zinthu zolengedwa za chirengedwe Chake, chifukwa ife sitikanakhoza kukhala achibale kumeneko. Chotero, Mulungu anadzakhala munthu, kuti munthu adzathe kukhala Mulungu, kudzakhala Mulungu. Ameni.

164 Ife, pokhala anthu, ochimwa, Mulungu anadzakhala wochimwa, anadzitengera machimo athu pa Iye. Wosadziwa machimo, komabe anali wochimwa chifukwa machimo athu anayikidwa pa Iye. Kuti ife. . .Iye anadzakhala ine, kuti ine ndidzakhale Iye. Mukuona? Iye anadzakhala wochimwa, kuti ine ndidzakhale mwana wa Mulungu. Iye anadzakhala wochimwa, kuti inu mudzakhoze kukhala mwana wa Mulungu. Ndipo tsopano ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, chifukwa Mulungu anapangidwa wachibale pamene Iye anadzatenga mawonekedwe a thupi lathu, anabadwa mwa mkazi. Mulungu! Osati munthu wina; Mulungu, Iyemwini.

165 1 Timoteo 3:16 anati:

> *. . .popanda kutsutsana chachikulu ndi chinsinsi cha umulungu:* pakuti *Mulungu* anawonetseredwa *mu thupi,* . . .Mulungu!
>
> *Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.*
>
> *Ndipo Mawu anasandulika thupi,* . . .

166 Mawu, anadzapanga munthu, anadzakhala wachibale. Iye anadzakhala munthu. Oh! Iye anadzakhala imfa, kuti kudzera mu imfa Yake ine ndidzakhoze kukhala Moyo. Iye anadzakhala wochimwa, kuti kudzera mu chirungamo Chake ine ndidzathe kukhala. . .kukhala ndi Moyo. Iye anadzakhala wosauka, kuti ine, kudzera mu umphawi Wake, ine ndidzathe kukhala wolemera. Iye anadzakhala chimene ine ndinali, kuti ine ndidzathe, kudzera mu chisomo Chake, ndidzakhale chimene Iye ali. Oh, mai! Kenako, mukakamba za mphamvu ya Mulungu! Tsopano, ndizo ndendende Malemba. Ndipo ndizo zimene Malemba amanena.

167 Kuti ife tidzathe kukhala. . .Ndi chikondi bwanji, Atate watsanulira pa ife, anatsanulira pa ife, kuti ife amene tinali ochimwa, alendo, otalikirana ndi Mulungu, tidzakhoze kuyandikira kwa Mulungu, poteropo kuti ife tidzakhale ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, osati antchito. Mpingo wa Amitundu sunakhalepo wantchito. Ayi, bwana. Mpingo wa Amitundu ndi mwana wamwamuna ndi wamkazi. Inu ndi

ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, amene mwalandira Mzimu Woyera. Tsopano, ngati inu muli gulu la Olipa, ndipo munapotoloka? Koma ngati inu mwapitirira mpaka ku Mzimu Woyera, inu mwadzakhala ana aamuna ndi aakazi.

168 Tsopano, ana aamuna ndi aakazi, ndani ali ndi mphamvu yochuluka pamaso pa Mulungu? Kodi Mngelo ndi chiyani? Mngelo ndi wantchito. Nkulondola uko? Iwo ndi antchito Ake. Inu ndi chiyani? Mwana Wake wamwamuna ndi wamkazi. Ndi ndani ali ndi mphamvu zambiri Kumwamba, ndiye, wochimwa amene wapulumutsidwa mwa chisomo, kapena Mngelowamkulu amene waima pambali Yake yakumanja? Wochimwa, amene wapulumutsidwa mwachisomo, ali ndi ulamuliro wochuluka Kumwamba kuposa Mngelowamkulu amene anayima pambali Pake, wopanda tchimo, chifukwa iye ndi mwana. Mwana amakhala ndi ulamuliro wochuluka kuposa wantchito, ndithudi.

Oh, ife timaiwala chimene ife tiri. Ife timaiwala, nthawi zambiri, chimene chinatipanga ife chimene ife tiri. Ife titatha kukhala chimene ife tiri, kenako tinaiwala momwe ife tinafikira kuno. “Pamene Mulungu Iyemwini . . . ”

> Oh, chikondi chofunikira bwanji chimene Atate
> Anapereka kwa mtundu wakugwa wa Adamu;
> Anapereka Mwana Wake yekhayo kuti adzavutike,
> Ndi kudzatiwombola ife mwa chisomo Chake.

Oh, momwe ife timadziwira!

> Pakati pa miyala yosweka ndi mlengalenga mwamdima
> Mpulumutsi wanga akuweramitsa mutu Wake nkufa;
> Chophimba chotseguka chinaulula njira
> Ku chisangalalo cha Kumwamba ndi tsiku losatha.
>
> Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndaima;
> Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.
>
> Pamene ndiyang’ana mtanda wodabwitsa
> Pamene Kalonga wa Ulemelero anafera,
> Ndimaona machimo anga onse kukhala chitayiko.

169 Uko nkulondola. Wina anati:

> Pokhala moyo, Iye anandikonda ine; pakufa, Iye anandipulumutsa ine;
> Poyikidwa mmanda, Iye ananyamulira machimo anga kutali;
> Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulere kwanthawizonse:

Tsiku lina Iye akubwera—oh, tsiku laulemelerolo!

170 Iyo yakhala ili mbalume ya Mpingo. Iyo yakhala ili mawonekedwe Ake. Iyo yakhala ili mtima Wake. Dziko ili lasambitsidwa ndi Magazi a Muwomboli Wachibale uyu, kuti adzawombole mtundu wakugwa wa Adamu.

171 Zindikirani, ndi Uyu apa, Muwomboli Wachibale. Tsopano, chinthu choyamba, Iye ankayenera kukhala munthu woyenera. Ndani amene anali woyenera mochuluka kuposa Khristu, kuposa Yesu? Ndiye, chinthu china, Iye ankayenera kukhala ndi ndalama. Iye ankayenera kuti adzakhale wokhoza kuchita izo. Iye anali mwini wa Miyamba. Iye anatsimikizira kuti Iye anatero. Iye ankatha kutenga mikate faivi ndi nsomba ziwiri, ndi kudyetsa faivi sauzande, kutenga mitanga faivi yodzaza ya zidutswa, pamapeto pake. Iye ankatha kupopa madzi mu chitsime ndi kuwasandutsa vinyo. Iye amakhoza kutenga nsomba kuchokera mnyanja, ndipo nkuchotsa ndalama mkamwa mwake, ya golide. Ameni. Iye sanali a . . .

172 Koma Iye anadzakhala wosauka, wopanda malo oti agonekepo mutu Wake. Iye anadzakhala Wachibale. Osati Wachibale kwa wolemera; Wachibale kwa anthu onse. Iye anatenga malo a muwomboli.

173 Ndiye kodi iye ankayenera kuchita chiyani? Kenako iye ankayenera kupanga umboni wa poyera. Mmawa wotsatira, Rute anati, kapena, Naomi anati, “Pumula, Rute, chirichonse chikhala bwino tsopano, chifukwa iwe wapeza chisomo pamaso pake.”

174 Mulungu, ndiroleni ine ndichite zimenezo. Ndiroleni ine ndipeze chisomo pamaso Pake. Ndiye pamene mmawa uzibwera:

Pamene lipenga la Ambuye lidzawomba, ndipo nthawi siidzakhalaponso,
Ndipo mmawa udzafika ku Muyaya, kowala ndi kokongola;
Ndipo pamene opulumutsidwa padziko adzasonkhana pa Gombe linalo,
Pamene mpukutuwo udzayitanidwa kutsidyako, ine ndidzakhala komweko.

175 Ndikupumula tsopano, ndikuyembekezera chiwombolo chathunthu. Zindikirani, ine ndiri nawo Iwo—chikole cha Iwo, tsopano. “Ndinatengera kunyumba balere wodzaza mpango. Ndinafikako kumeneko.” Iye anapereka balereyo kwa iye, anamuyeza iye, miyeso sikisi. Sikisi, amatanthauza, “zaka sikisi sauzande za kukhalapo kwa dziko lapansi.” Tsiku la munthu ndi sikisi. Munthu analengedwa pa tsiku la sikisi. Padzakhala zaka sikisi sauzande zimene dziko linalengedwa, mu cha seveni sauzande Mulungu anapuma. Zaka sikisi sauzande Mpingo udzagwira ntchito motsutsana ndi tchimo, ndi Mphamvu ya

Mulungu ya mikate iyi ya balere, ndipo kenako nkupita mu Mpumulo Wamuyaya. Kulondola. Kupumula, kudikirira. Miyezo sikisi ya balere wabwino, kuti amusunge iye kufikira nthawi ya chiwombolo chake chathunthu. Ndine wokondwa kwambiri kusangalala nazo.

176 Tsopano, mwamsanga, tiyeni tifike ku mapeto ake. Tsopano ife tikupeza, tsopano, kuti, mmawa wotsatira, pamene iye anadzuka, iye anali wokondwa, akudikirira. Ndipo mwamunayo anabwera. Iye anapita kumeneko. Iye anali ndi wachibale wina amene kwenikweni anali ndi kusankha pa mkaziyo, poyamba. Kodi ndiri ndi nthawi yoti ndizipeze zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino, miniti yokha, ndipo ife titenga gawo la izo, mulimonse.

177 Wotsatira uyo mu fanizo, amene anali ndi kusankha pa inu, anali mdierekezi, chifukwa inu munali mutachimwa. Ndipo poyamba inu munali ake a iye, chifukwa, inu munali, ndinu katundu wake. "Pakuti inu munabadwa mu tchimo, kuwumbidwa mu kusaeruzika, munabwera mdziko mukuyankhula bodza." Ndipo iye sakanakhoza kuwombola zimenezo. Mukuona? Iye sakanakhoza kuwombola zimenezo. Chotero, Khristu anabwera ndipo anadzapangidwa kukhala munthu, kuti adzachotse machimo athu, kuti adzatiwombole ife. Kodi inu mukuziwona zimenezo? Ndipo munthu winayo sakanachita zimenezo. Mdierekezi sakanakhoza kufera machimo, chifukwa iye anali wopotoza yemweyo amene analipanga tchimo. Mukuona? Iye sakanakhoza. Iye akanawononga cholowa chake, munthu winayo. Ndipo Satana akanawononga chake, chifukwa iye ndi mdierekezi. Iye sakanakhoza kudzakhala mdierekezi wina, kuti adzamuchotse mdierekezi, mdierekezi woyamba. Iye sakanakhoza kudzakhala tchimo, chifukwa iye anali kale tchimo. Koma, Khristu, pokhala wopanda tchimo, anadzakhala wochimwa. Iye anakhoza kutiwombola ife. Aleluya! Ife ndi owomboledwa. Ife ndi *owomboledwa*, zikutanthauza, "kubwezeretsedwanso." Ife ndi owomboledwa.

178 Chotero, mmawa wotsatira, ndiye iye ankayenera kuti apange umboni wa pa anthu onse. Iye anapita uko ndipo anakakumana ndi munthu ameneyu pa chipata, pamaso pa akulu akulu. Ndipo iwo ankayenera kuti akhale pa malo pa anthu onse. Ndipo iye anamuyang'ana iye pa nkhope. Iye anati, "Kodi iwe ungathe kumuwombola iye?" Tsopano, ngati iye akanati amuwombole poyamba Naomi, kuti amutenge Rute; ndipo Khristu ankayenera kuti awombole mpingo wa Chiyuda, poyamba, ndi cholinga choti amutenge Mkwatibwi wa Amitundu. Iye anabwera ndi Naomi, ngati mlendo wochokera ku dziko lina, wachi Moabu, achikunja. Ndicho chimene ife tinali, Amitundu, achikunja. Ndipo kumbukirani, iye anka— iye ankayenera kuti amutenge Naomi. Ndipo pamene iye

anamutenga Naomi, iye anatenga zonse zomwe Naomi anali nazo.

179 Kumbukirani, pamene Khristu anabwera, Iye sanayankhule konse za Mpingo wa Amitundu. Izo zinali, kupita kwa Ake omwe, "Iye anabwera kwa Ake omwe. Ake omwe sanamulandire Iye." Iye nthawizonse anali kwa Ake omwe. "Musapite mnjira ya Amitundu. Musapite ku Samariya, koma makamaka mupite kwa nkhosa zotayika za Israeli. Ndipo pamene inu mukupita, mukalalikire Uthenga, mukachiritse odwala, mukawukitse akufa, mukatulutse ziwanda. Mwaulere monga mwalandirira, mukapereke mwaulere." Nkulondola uko? Anawatumiza iwo, awiri awiri. Mupite poyamba...Ndipo Iye ankayenera kuti awuwombole mpingo umenewo. Ndipo pamene Iye anawombola mpingo umenewo, Iye anamtenga Mkwatibwi wa Amitundu. Ameni. Kumeneko kunali kukambirana mmenemo. Mukuona? Iye anamtenga Mkwatibwi pamene Iye anawuwombola mpingo.

180 Tsopano, Boazi, iye ankayenera kulengeza poyera...Iye anati, "Kodi mungathe kumuwombola iye?"

Iye anati, "Ayi."

181 Kenako iye ankayenera kuti apange umboni wa pagulu pa anthu. Iye anavula nsapato yake, ndipo anaiponyera iyo pa iye. Anati, "Ndi zimenezotu. Mulole Israeli yense adziwe kuti ine ndamuwombola Naomi, ndiponso ndikumutenga Rute." Ameni. "Ine ndikumutenga Rute kukhala mkwatibwi wanga." Anali ndani ameneyo? Mbuye wa zokolola. Ameni. Ndi uyo pamenepo. "Ine ndikumuwombola Naomi, ndipo ndikumutenga Rute. Ndipo Rute akhala mkwatibwi wanga."

182 Kodi iwo anati chiyani? "Mulole iye akhale monga—monga Leya ndi Rakelo ndi iwo, awukitse masauzande," ndipo iye watero, uko nkulondola, "kwa Israeli. Mulole iye akhale mwanjira imeneyo." Ndipo, taonani, iye anapanga mayeso, umboni wa pagulu pa anthu.

183 Kodi Yesu anachita chiyani, kuti achite izo? Iye anapanga umboni wa pagulu pa anthu. Pamene, Satana sakanatha kufera machimo chifukwa iye anali wochimwayo. Iye ndi tate wa tchimo. Koma, Yesu, Mmodzi wosalakwayo, Mulungu wa Kumwamba, Yemwe sankayenera kufa, anadzabwera pansi ndipo anadzapanga umboni wa pagulu pa anthu pa kufa, ananyamulidwa mmwamba pakati pa miyamba ndi dziko lapansi. Umboni wa pagulu pa anthu; anamuvula zovala Zake pa Iye, ndipo anapachikidwa pakati pa miyamba ndi dziko lapansi, mwa manyazi. Ndipo anafa, imfa yochimwa, yochititsa manyazi, kuti adzatiwombole ife. Umboni wa pagulu pa anthu! Ameni.

184 Kodi Iye anachita chiyani? Anakankhira uko chirungamo Chake chomwe; anakankhira uko ulemelero Wake womwe. Anakankhira... "Ine ndiri ndi mphamvu. Ine ndikanayankhula kwa Atate Anga, ndipo nthawi yomweyo Iye akananditumizira

Ine magulu twente a Angelo.” Iwo akanadzakhoza kusintha chonsecho. Mngelo mmodzi akanakhoza kuchita zimenezo. Iye akanakhoza kuitana magulu twente. Amenewo akanakhala pafupifupi Angelo forte sauzande. Kodi iwo akanakhoza kuchita chiyani? Iye anati, “Ine ndikanakhoza kuyankhula kwa Atate Anga, nthawi yomweyo, zimenezo ndi pakali pano, Iye akananditumizira Ine magulu twente. Magulu a Angelo abwera kuno ndi kudzalanda izi.” Kodi mmodzi akanadzatani? Mmodzi akanadzawononga dziko lapansi, mu mphindi. Tangoyang’anani, Iye anali ndi masauzande amene akanakhoza kubwera. Mukuona? Koma Iye anazikankhira uko zimenezo. Iye anaziyika izo pambali. Iye anayika ulemelero Wake wonse, chirichonse, pambali, ndipo anadzakhala wochimwa ndipo anafera inu ndi ine.

185 Tsopano, potseka, ife tikhoza kunena izi, potseka. Iye anachita—iye anachita zimenezo. Kenako iye anamutenga Rute, ndipo anamukwatira iye. Ndipo anadzabereka mwana wamwamuna dzina lake Obedi. Obedi anali bambo ake a Jese. Jese anali bambo ake a Davide, yemwe anali bambo a Khristu, ameni, bambo a Ambuye Yesu.

186 Kodi inu simukuona? Kudzera mu chirungamo chimenecho, kudzera mu chisankho chachindunji chimenecho, Iye anadzakhala Muwomboli Wachibale wathu. Mulungu anadzakhala wachibale kwa ife, kuti abwere pansi ndi kudzapangidwa monga ife, munthu, kudzamva njala, kudzamva ludzu. “Ine ndikumva ludzu. Ndipatseni Ine chakumwa.” Ndipo iwo anayika vinyo wosasa mkamwa Mwake, ndulu. Iye anamva ludzu monga ife timachitira. Iye ankadziwa kuchita wopanda.

187 Iye ankadwala monga ife timachitira. Iye anati, “Kodi iwo sanena kwa Ine fanizo lakale, ‘Sing’anga, dzichiritse wekha’?” Koma mphamvu Zake zazikulu sizinali za Iyemwini. Iye anali ndi mphamvu yochitira izo, koma Iye sakanakhoza kuigwiritsa ntchito pa Iyemwini. Ayi.

188 Winawake anati kwa ine, tsiku lina, anati, “M’bale Branham, chirichonse chisanachitike, inu mumadziwa zonse zomwe ziti zikuchitikireni inu.”

189 Ine ndinati, “Mphatsoyi si ya ine. Ine sindingakhoze kuigwiritsa ntchito kwa inemwini.” Iyo ndi yanu. Inu ndi amene mumapeza phindu, osati ineyo. Ine ndi mtumiki chabe wa anthu a Mulungu, kwa inu.

190 Mlaliki ndi mtumiki wa anthu. Iye amangodzigwirizitsa yekha pamenepo. Monga kakombo wa mmunda, njuchi imaulukira mkati, imatenga gawo lake. Njuchi ya uchi imawulukira ndi kutenga lake. Wodutsa amatenga lake, ndi chirichonse. Iye amagwira ntchito, usana ndi usiku, kuti asunge kuwala kwake. Ndipo mtumiki wa Uthenga amachita chinthu chomwecho; amayenda mu mzere wa Mulungu. Amagwirizitsa

umboni wake moona, kuti dziko likhoze kudya nawo za iye, mwaona, Bambo M'busa Lily. Iye ndi wabwino. Yesu anati, "Tamulingalireni iye. Solomoni sali ngati iye." Uko nkulondola. Dokotala Lily, ine ndikuganiza inu nonse mukumudziwa iye. Mukuona?

191 "Talingalirani maluwa a kuthengo, momwe iwo amavutikira ndi kupota, chonchobe. Ine ndikuti, ndipo, komabe, Solomoni, ulemelero wake wonse..." Kakombo amachita kuvutikira, usana ndi usiku, kuti apeze kuwala koti kusunge zovala zake, kusunge mafuta onunkhira ndi zinthu zizipitirira. Ndipo ena...Iye amangodzitsegula yekha, ndipo iwo amabwera ndipo amazichotsa izo mwa iye. Njuchi ndi ntchentche, ndi chirichonse, zimabwera, chabwino kapena choipa, zimangotenga kwa iye.

192 Umo ndi momwe mtumiki amakhalira, wa Khristu, mtumiki wa Chikhristu; amadzitsegula yekha, "Mudzangotenga kuchokera kwa ine, dziko lapansi." Palibe kanthu kwa iyemwini. Ndi za ena. Chimenecho ndi chimene Khristu anadzakhala pamene Iye anadzakhala wachibale kwa ife. Iye anadzakhala munthu, kuti dziko lidzathe kutenga za chirungamo Chake, mwaona, ndi kudzapangidwa ana a Mulungu.

193 Tsopano, kodi iwo anachita chiyani? Iwo anakwatirana, ndipo kudzera mu chimenecho panabwera chinthu chachikulu ichi. Kenako Rute analipidwa, pomutenga Khristu...kapena pomutenga Boazi kukhala mwamuna wake. Chimene, Mpingo udzalipidwa, pamene Kudza kwa Ambuye kudzabwera, mmawa wowala ndi wopanda mitambo uwo. Ife tikupumula, tikuyembekezera tsopano. Iwo udzabwera. Tsopano, chifukwa chiyani? Iwo wawomboledwa.

194 Tsopano, chobwereza chimodzi china ine ndisanachoke, kuti tiyambe mzere wa pemphero. Chobwereza chimodzi china. Ine ndinafufuza, mmawa uno, mawu akuti *kuwombola.* Ine basi...Mundikhululukire ine, abale anga achi Arminian, koma ine ndikungoyenera kuyikamo ichi; osati kukupwetekani, koma kuti ndingokupangitsani inu kuganiza. Muyang'ane chimene *chiwombolo* chimatanthauza. Chiwombolo, kwenikweni chimagwiritsidwa ntchito, mu liwu la Chigriki, ngati kumutenga kapolo kumuchotsa ku msika. Ine sindingathe kulitchula liwu la Chigrikilo pakali pano, koma ilo limatanthauza, "kumutenga kapolo kumuchotsa ku msika," ku*wombola.*

195 Munthu wachita chinachake cholakwika, chotero, iye, mbuye wake anamugulitsa iye mu ukapolo, makamaka kufikira imfa. Ndipo iye ali mu msika, iye ndi kapolo. Koma munthu akubwera, munthu woyenera amene angathe kuchita zimenezo, ndipo akumupeza munthu uyu, ndipo akupeza chisomo pamaso pake, iye akumuwombola iye. Uko ndi kumuchotsa iye ku msika wa akapolo, ndipo

nkumutengera iye kwa iyemwini. Zindikirani. Ndipo kapolo ameneyo, akangowomboledwa kamodzi, sangagulitsidwenso pa msika. Ameni. Sangagulitsidwenso kachiwiri. Iye amaikidwa chizindikiro. Ndipo ngati iye anaganiziridwapo mokwanira, nthawi yina, kuti awomboledwe, palibe amene angakhoze, konse, kumugulitsa iye kachiwiri ngati kapolo.

196 Oh, mathokozo akhale kwa Mulungu, kuti pamene munthu abwera kamodzi kwa Khristu ndipo wawomboledwa ndi Magazi amtengo wapatali, mdierekezi sangathe kukupanga iwe kukhala kapolo kachiwiri. Ndiwe wotetezeka mu Magazi a Yesu Khristu mpaka tsiku la chiwombolo chako. Kapolo, fufuzani zimenezo mu Eksodo, ndipo mupeze ngati amenewo si malamulo Achilevi. Ine ndikutanthauza, mu Levitiko, muwone ngati amenewo si malamulo. Kapolo, akangowomboledwa kamodzi, sangagulitsidwenso ngati kapolo. Uko nkulondola.

197 Oh, ndine wokondwa kwambiri! Ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti Muwomboli Wachibale wathu, kuti Mulungu wa Kumwamba, Yemwe anali Mzimu, anatsika ku dziko lapansi ndipo anasandulika thupi; anapangidwa momwe ine ndiriri, anadzapangidwa momwe inu muliri; ndipo anavala mawonekedwe a thupi lochimwa, osadziwa tchimo, kuti machimo athu adzakhale pa Iye; ndipo anadzakhala wachibale kwa ife, anachita umboni wa pagulu pa anthu wa kufa, akulipira mtengo wathunthu.

198 Ndipo Mzimu wa Mulungu ukuchitira umboni. Kachisiyo anang'ambidwa, chophimbacho, kuchokera pamwamba kufika pansi. Osati kuchokera pansi kupita pamwamba, koma kuchokera pamwamba kupita pansi; zinawonetsera kuti anali Mulungu, Mwiniwake, anaching'amba icho motsegula, kuchokera Kumwamba. Anaching'amba icho kuchokera pamwamba mpaka pansi, ndipo anatsegula njira. Ndipo miyala ya nsembe inatembenuzika, ndipo mphezi inadutsa mu miyamba yakuda, yokwiya. Dzuwa linakalowa pakati pa tsiku. Nyenyezi zinakana kuwala. Ndipo chirichonse chinaperekera umboni, "Ife tawomboledwa." Aleluya!

Tiyeni tipemphere. [M'bale akupereka mawu a uneneri—Mkonzi].

199 Ndi mitu yanu yoweramitsidwa tsopano, mphindi chabe. Amenewo anali mawu a uneneri, akuyitanira kwa mpingo, utatha Uthenga.

200 Tsopano ngati alipo ena pano amene samamudziwa Iye, miyoyo yanu si yabwinobwino, inu mukuitanidwa tsopano kuti muyime pano mu kukhalapo kwa omvetsera awa, nkhope ya Mulungu, kuti mumulandire Iye ngati Mpulumutsi wanu. Madzi ali mu dziwe a ubatizo. Ngati winawake akuyembekezera kuti ayambe msonkhano wa ubatizo, nthawi yomweyino.

201 Pamene tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, titenga kanthawi tsopano poyimba *Ine Ndikupyolatu*, ndi mitu yanu yoweramitsidwa tsopano.

> Ine ndikupyolatu, inde, ine ndikupyolatu,
> Ndilipira mtengo wake osawona chimene ena akuchita,
> Ndidzayenda njira ndi onyozeka apang'ono a Ambuye,
> Ndayamba ndi Yesu, ndipo ndikupyolatu.
>
> Ine ndipyolatu, inde, ine ndipyolatu,
> Ine ndi . . .

Kodi inu mukutanthauzadi zimenezo kwenikweni tsopano? Ngati inu mukutero, bwerani kuno ndipo mudzayime.

> . . . chirichonse chimene ena akuchita,
> Ndidzayenda njira . . .

Kodi mwakonzeka kupatuka?

> . . . a Ambuye . . .

Monga Naomi wakale?

> Ndayamba ndi Yesu, ndipo ine ndikupyolatu.
>
> Kuchokera modyera ziweto ku Betelehemu kunabwera Mlendo,
> Padziko lapansi ndilakalaka kukhala monga Iye;
> Kudutsa monse mu ulendo wa moyo kuchoka mdziko kupita ku Ulemerero
> Ine ndikungopempha kuti ndikhale monga Iye.
>
> Kukhala monga Yesu . . .

Inu mukufuna kukhala monga Muomboli wanu?

> . . . monga Yesu,
> Padziko ndilakalaka kukhala monga Iye;
> Kudutsa monse mu ulendo wa moyo kuchoka mdziko kupita ku Ulemelero
> Ine ndikungopempha kukhala monga Iye.
>
> Walirani pa ine, Ambuye, walirani pa ine,
> Mulole Kuwala kochokera ku nyumba ya Kuwala kuwalire pa ine;
> Walirani pa ine, Ambuye, walirani pa ine,
> Mulole Kuwala kochokera ku nyumba ya Kuwala kuwalire pa ine.
>
> Kukhala monga . . .

Kodi alipo wina aliyense amene inu mukanafuna kuti mufanane naye, kupatula Iye? Kodi winawake sangabwere tsopano ndi kudzagwada apa ndi mtsikana uyu, pamene iye akugwada? Kutenga, monga Rute wakale, kutenga njira yake mmawa uno.

. . . monga Iye;
Kudutsa monse . . . mdziko ku Ulemelero,
ine ndikungopempha kukhala monga Iye.

Kungokhala monga Yesu . . .

Winawake abwere tsopano. Bwerani pansi apa ndipo mudzagwade pansi, monga dona uyu wachitira apa. Kodi inu mwayamba? Kodi inu mungayike manja anu mwa Ake?

. . . Ine ndikukhumba kukhala monga Iye;
Kudutsa monse mu ulendo wa moyo kuchokera
mdziko kupita ku Ulemelero,
ine ndikungopempha kukhala monga Iye.

[M'bale Branham akung'ung'uza *Kukhala Monga Iye*—Mkonzi].

202 Atate Athu Akumwamba, pamene mpingo ukung'ung'uza nyimbo iyi, "kukhala monga Yesu," mkazi uyu, mmawa uno, watulukira poyera, monga Rute. Ina Bell, akubwera ngati Rute wakale. Ziribe kanthu kuti mtengo wake ndi wotani, iye wabwera kudzalipira iwo. Ziribe kanthu chimene . . . momwe iye angasekedwere, kapena kusereulidwa, iye akutenga malowo tsopano, wayima apa, akuvomereza machimo ake. Wagwada pansi, akuika chizindikiro pa malo amene Ambuye wamkulu wa zokolola anagona pa mtanda. Ndipo pamenepo kuti alandire Mzimu Wake, chisomo Chake chimene chinayankhula kwa iye pamene Mawu amapita patsogolo, monga Naomi wakale, akulondolera. Ndipo Iwo unakhudza woyenera, malo oyenera. Ndipo tsopano iye akubwera kudzatenga malo a wokhulupirira, atagwada pa mtanda, pamenepo pamene iye akuulula machimo ake, wayika pambali zinthu zakale zonse za moyo, ndipo wakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu.

203 Ife tikupemphera, Atate, mmawa uno, kuti munthu aliyense wotalikitsidwa mchipinda chino, mwamuna aliyense, mkazi, mnyamata, kapena mtsikana, yemwe samakudziwani Inu, musalole Mawu awa adutse, Ambuye. Ife sitikudziwa basi ora limene ife titi tidzabwere mu Chiweruzo. Izo zikhoza kukhala lero kuti ambiri a ife tikuyenera kubwera. Mwinamwake tisanafike kwathu, ngozi ichitika. Mulole . . . Vuto la mtima likhoza kutikantha ife. Ife sitikudziwa. O Mulungu, tiloleni ife tikonzekere, ora lino, pamene Mzimu uli pano, pamene ife tiri ndi umboni kuti Iye ali pano, pamene Mulungu wa Kumwamba, mu chifundo Chake chonse chopanda malire, ali pano kuti atitengere ife mkati.

204 Tipatseni ife chisomo Chanu, Ambuye. Mutumize ena, mmawa uno, ku guwa, ndipo amulandire Khristu ngati Mpulumutsi, monga mkazi uyu akuchitira tsopano. Perekani izi, Ambuye. Muchitireni chifundo, podziwa kuti anthu ake . . . Mchimwene wake wakhala pano pa nsanja ndi ine. Mchemwali wake, Wood, wakhala kumbuyo uko; amayi ndi

adadi akhala apa. Ambuye Mulungu, ine ndikupempherera chifundo. Mupereke izi, Ambuye. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza mu mtima mwanga. Ine ndikupempha kuti kukhetsa Kwanu kwa Magazi Anu, mu chifundo, kubwere tsopano pa ora lino. Mupereke izi, Ambuye. Mupereke, pamene ife tikuyembekezera ena, mulole enawo abwere, nawonso, Atate, ndipo ayanjanitsidwire kwa Mulungu kudzera mwa Khristu.

205 Ndipo tsopano, pamene ife tikuyembekezera tsopano ndi kudabwa, ife tiyimba kachiwiri.

> Muwalire pa ine, O Ambuye, muwalire pa ine.
> Mulole Kuwala kochokera ku nyumba ya Kuwala kuwalire pa ine.

Chabwino. Eya.

> Muwalire. . .

Kodi pangakhale wina amene angabwere?

> . . .muwalire pa ine,
> Mulole Kuwala kochokera ku nyumba ya Kuwala kuwalire pa ine;
> Muwalire pa ine, Ambuye, muwalire pa ine,
> Mulole Kuwala Kwanu kochokera ku nyumba ya Kuwala, kuwalire. . .

Kodi Iko kundipanga ine chiyani?

> Kukhala monga Yesu, kukhala monga Yesu,
> Padziko ndilakalaka kukhala monga Iye;
> Kudutsa mu ulendo wa moyo kuchoka mdziko kupita ku Ulemelero
> Ine ndikungopempha kuti ndikhale monga Iye.

206 Atate Mulungu, umenewo moonadi ndi umboni wathu. Ambuye, ife tikufuna kuti tikhale monga Iye, ofatsa ndi odekha, odzichepetsa, okoma, nthawizonse okhululukira iwo amene akumuchitira Iye zoipa ndi kulakwitsa. Ife—ife tikufuna kuti tikhale mwanjira imeneyo. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha mkazi uyu amene anabwera mmawa uno. Kodi ife tikudziwa bwanji chimene moyo uwu udzakhale, pakapita kanthawi? Mwinamwake kudzera mu zolakwitsa zake zonse ndi zinthu mmoyo, monga ife tonse talakwitsira, kuwona izo zitayikidwa pansi pa kusefukira mmawa uno. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti mkazi uyu azikhala moyo wodzipereka umene utatsogolere oyanjana nawo ake onse ku chomuchitikira ichi. Mulole iye asasiyire apa, koma apitirirebe ku dziko lolonjezedwa, akuika chizindikiro pa malowo ndi kugona pansi, akulandira Mzimu Woyera pamenepo. Mupereke izi, Ambuye.

207 Ngati alipo enanso muno, Atate, amene akanabwera, ndipo sanatero, mulole Mzimu Wanu usawasiye iwo. Mulole iwo asakhale ndi mpumulo, usana kapena usiku, mpaka iwo atabwera, nawonso, nkudzapanga chisankho chomwechi. Osati

kuti ndikhale wankhanza, Ambuye, koma, O Mulungu, podziwa chimene iwo akuchisowa. Podziwa mmene ziti zidzakhalire pa Tsiku limenero, kudzamumva Iye akunena, "Chokani kwa Ine, inu akuchita kusaeruzika. Mmawa umenewo, pa Eighth ndi Penn Street, ine ndinakuitanani inu, ndipo inu simunabwere." O Mulungu, ndi ora loyipa bwanji limene ilo lidzakhale kwa iwo, pamene ife tidzayezedwe pa sikelo ndi kudzapezeka operewera. Atate, mupereke kuti izo zisadzabwere konse kwa aliyense mu Kukhalapo Kwauzimu. Mulole iwo onse apulumutsidwe. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Ameni.

208 Ife tikufuna kumuthokoza Ambuye, mmawa uno, chifukwa cha ubwino Wake ndi chifundo. Ine ndikukuthokozani inu nonse chifukwa cha chipiriro chanu, poyembekezera ndi ine nthawi yayitali chomwechi.

Mlongo Ina Bell. Ine. . . Mlongo Wood, ameneyo ndi mchemwali wanu, M'bale Charlie. Zimene iwo akhala akuzipempherera, ndi zimene ife takhala tikuzipempherera, kwa nthawi yayitali. Mlongo Ina Bell, kodi mungaimirire, mphindi chabe? Ameneyo ndi wa Mlongo Wood. . . Trastii wathu kuno ku tchalitchi, ameneyo ndi mlamu wake wamkazi, amene wamulandira Yesu monga Mpulumutsi wake mmawa uno. Ndipo ndi mapemphero angati akhala. . . Mulungu akudalitseni inu, Mlongo Ina Bell. Ine ndikuganiza kuti ndikutchula dzina lanu molondola. Nkulondola uko? Mulungu nthawizonse azikudalitsani inu, mlongo wokondedwa. Ndipo ngati inu simunabatizidwepo konse mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikukulimbikitsani inu kuti muchite izo, ndi kudzalandira Mzimu Woyera.

209 Mulungu nthawizonse azikhala ndi iwe, adalitse mwamuna wako wofunikira pamenepo. Ine ndinakomana naye iye, masiku angapo apitawo. Ngati sindikulakwitsa, dzina lake ndi Stanley. Nkulondola uko? Stanley. Mulungu akudalitse, Stanley. Kunyumba ndi kokoma, koma ndikukhulupirira kuti kukakhala kokoma kuposa kale. Mulungu nthawizonse azikhala ndi inu nonse, ndipo—ndipo akupatseni inu chisomo Chake ndi chifundo, masiku onse a moyo wanu. Ndipo utsatirebe ndi Ambuye. Ukhale monga Rute tsopano, Ina Bell, umamatire bwino kwa Iwo. Uzingopitirira kusunthira patsogolo. Nthawizina zizikhala zovuta, ndipo njira zizikhala za mdima. Koma, kumbukira, uzingoyang'ana pansi moloza pansi, ndipo kenako uziyang'ana mmwamba moloza thambo, iwe udzapeza chidindo cha mapazi a Magazi omwe amatsatira njira yonseyo. Iye adzatsogolera njirayo.

210 Tsopano, oh, ndi masana kale, thwelofu koloko. Kodi inu mukufunabe kukhala ndi mzere wa pemphero? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

211 Billy, kuti, mtundu wanji. . .? Kodi iye anapereka makadi

apemphero? Ine—ine sindina...Ine ndikukhulupirira iye anandiuza ine kuti iye anapereka pemphero...Chabwino, anali chiyani iwo? Winawake andiuze ine chimene chilembo ndi manambala zinali. [M'bale akuti, "Apo iye akubwera."—Mkonzi]. Chiyani? [M'bale Billy Paul akuti, "B."] B. B, wani mpaka handirede? Fifite mpaka handirede. Chabwino. B, nambala wani. Iwo ali...

212 Tsopano, tiri ndi gulu, chotero sitingathe...Ife tiwaimitsa iwo onse, ndipo ife tizingowadutsitsa iwo pomwepo, pamene ine ndikuwapempherera iwo.

213 Tsopano, ndi angati amene sanayambe awonapo umodzi wa mizere ya pemphero? Tiyeni tiwone manja anu, simunakhalepo mu umodzi wa misonkhano yanga, ku mzere wa pemphero. Oh, mai! Ambiri a inu.

214 Chabwino, tsopano, ife titha kungowapempherera anthu, kapena ife tikhoza kukhala ndi kuzindikira zamumtima, kapena osakhala ndi mzere wa pemphero konse; kungowayitana iwo pomwepo, mwa omvetsera. Izo ziribe kanthu. Mzimu Woyera uli pano. Inde, bwana. Koma tiyeni tikhale titayima pa mzere wa pemphero.

Nambala wani, ndani ali ndi nambala wani, khadi la pemphero B? Namba-...Fifite. Ine ndikupepesa. Palibe amene ali nalo, ndithudi. Chabwino. Khadi la pemphero fifite, ndani ali nalo? Bwerani kuno, bwana. Khadi la pemphero thuu...

Fifite-wani, fififte-thuu. Khadi la pemphero fifite-thuu. Chabwino. Fifite-firii. Fifite-firii. Chabwino. Fifite-foro.

Bwerani mbali iyi, pomwe *pano*. Ngati muli kumbuyo, bwerani mbali iyi, cha *apa*.

Fifite-wani, fifite-thuu, fifite-firii, fifite-foro. Ndani ali ndi fifite-faivi, khadi la pemphero fifite-faivi? Dona, pomwe *apa*. Khadi la pemphero fifite-sikisi.

Imirirani, mmbali mwa khoma, cha *pamenepo*, ngati mungathe.

Fifite-seveni, fifite-eyiti, fifite-naini, sikisite. Sikisite-wani, sikisite-thuu, sikisite-firii, sikisite-foro, sikisite-faivi.

Busty, tatembenuka pomwepo udutse mu kanjira ako pomwepo apo, m'bale, pomwepo *apo*. Chabwino. Tembenuka pomwepo udutse.

Ndi angati alibe khadi la pemphero, ndipo inu mukufuna kuti Ambuye akuchiritseni inu? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino. Ndizo zonse zomwe inu muyenera kuchita, mungokhulupirira izo tsopano. Mungokhulupirira. Chabwino.

Fifite-sikisi. Kodi ndiri nalo? Fifite-seveni, fifite-eyiti, fifite-naini, sikisite. Aloleni iwo ayimirire.

Sikisite-wani, -thuu, -firii, -foro, -faivi. Aloleni iwo ayimirire. Sikisite-sikisi, sikisite-seveni, sikisite-eyiti, sikisite-naini, sevente. Aloleni iwo ayimirire.

Sindikufuna kuti iwo onse athamangire pa nthawi imodzi, ndi chifukwa chake ndikuitanira nambala, mpaka sevente.

Sevente mpaka eyite, imirirani. Bwerani kuno, mbali *iyi*, sevente mpaka eyite. Chabwino. Wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, eyiti, naini. Chabwino.

Eyite mpaka nainte, imirirani cha *apa*. Doc, iwe uwathandizire iwo kumbuyo uko, ngati ungathe. Eyite mpaka nainte, imani cha ku mbali *iyi*.

Nainte mpaka wani handirede, imani cha ku mbali iyi, cha *apa*. Chabwino.

215 Pamene iwo akufola, ine ndikufuna kuti ndiwufunse mpingo chinachake. Kodi ndi alendo angati ali muno, amene sanakhalepo mu umodzi wa misonkhano yanga kale? Ndi angati a inu? Ndi angati amene akudziwa kuti palibe munthu angathe kuchiritsa wina, osati ngakhale kwa dokotala? Ayi, bwana. Dokotala si mchiritsi. Iye amangothandizira chirengedwe. Mulungu ndiye mchiritsi. Mukuona? Dokotala akhoza kuwukonza nkono, koma sangathe kuwuchiritsa nkono. Dokotala akhoza kuchotsa thumbo, koma osati kuchiritsa malo amene wadulapowo. Dokotala akhoza kuzula dzino, koma osati kuletsa magazi kutuluka, kapena kulichiritsa ilo. Mulungu amayenera kuti achite zimenezo. Chabwino.

216 Ndi angati amadziwa zimenezo, pamene Yesu anali pano pa dziko lapansi, kuti Iye sankadzinenera kukhala mchiritsi? Iye anali Munthu. Iye anati, “Si Ine amene ndimachita ntchitozo, koma Atate Anga amene akukhala mwa Ine, Iye amachita ntchitozo.” Nkulondola uko? Ndi angati amadziwa, pamene Iye anali kuno, chiyani, motani. . .Ndi utumiki wamtundu wanji umene Iye anali nawo pamene Iye anali kuno? Iye ankachita chimene Atate ankamuwonetsera Iye kuti achite. Ndi kulondola uko? [“Ameni.”] Kodi ndi angati akudziwa, akudziwa zimenezo? Yohane Woyera 5:19, Iye anati, “Indetu, indetu, Ine ndinena kwa inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene Iye awawona Atate akuchita.” Nkulondola uko? [“Ameni.”] “Chimenecho Mwana amachita, chimodzimodzi.”

217 Tsopano, ndiye, kodi Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo, ndi mtima wanu wonse? [“Ameni.”] Iye ali yemweyo dzulo ndi kwanthawizonse. Kodi mukukhulupirira, kuti, Yesu Khristu pokhala yemweyo dzulo ndi kwanthawizonse, kuti izo zimatanthauza kuti Iye alidi yemwe yemweyo? [“Ameni.”] Chabwino.

218 Kodi Iye ali yemweyo chotani? Yemweyo mu mfundo iliyonse. Nkulondola uko? Iye ndi Mulungu yemweyo, Mchiritsi yemweyo,

a—Mpulumutsi yemweyo. Iye ndi yemweyo, maganizidwe omwe womwewo. Ndizo zonse yemweyo. Nkulondola uko? Yemweyo. Chabwino. Ndiye, ngati Iye anali yemweyo, ndipo ali yemweyo, Iye adzachita ndi kupanga momwemo. Nkulondola uko? Tsopano, ndi angati akudziwa zimenezo kuti ndi Choonadi?

219 Ine ndingotenga kamphindi pano. Ine ndikudikirira. Zimenezo sizikuwoneka, kwa ine, ngati kuti ndi anthu fifite ayima pamenepo. (Wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni, leveni, thwelofu, sartini, fortini.) Ayi. Ena a iwo mwinamwake apita kwawo, mofulumira. Ine ndinawawona anthu ena akuchoka kumbuyo uko. Chabwino, basi mzere wawung'ono, waufupi. Ndi angati akufuna kukhala ndi uwu? Kodi alendo angati kwa ine, mu mzere umenewo? Mukweze mmwamba dzanja lanu, akudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu. Mukweze mmwamba langa . . . dzanja lanu.

220 Kodi ndi angati kunja uko, alendo, akudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu? Mukweze mmwamba dzanja lanu, amene mukudwala. Chabwino. Ndi angati akufuna kuti awone mzere wa kuzindikira zamumtima, kuchitira kuti tingofulumira ndi kutsiriza? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Kodi mungafune . . .? Tsopano, ziribe kanthu. Ine ndikhoza kungowapempherera iwo, kuwabweretsa iwo kuti adutse mzere. Kapena, akhoza kukhala pansi, kungopita ndi kukakhala pansi. Ziribe kanthu. Mzimu Woyera ukhoza kuzindikira zimenezo, chimodzimodzi basi. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

221 Tsopano, ndiye, ngati izo ziri chomwecho, ndiye mungokhala chete, mphindi yokha. Kukuda pang'ono, chotero mungokhala bata, mphindi yokha. Ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake tsopano.

222 Ine ndikhoza kukhala pa choyankhulira cholakwika apa. Ziwiri zonsezo ziri bwinobwino? Ziwiri zonsezo ndi zolumikizidwa, chabwino, *ichi* apanso? [M'bale akuti, "Inde."—Mkonzi]. Chabwino.

223 Tsopano, mungokhala chete, kwa mphindi. Ine ndiyang'ana pansi pamzere uwu, ndiwone ngati ndikumudziwa aliyense.

224 Ine ndikumudziwa mwamuna uyo wayima pomwe *apo*. Tsopano, ine ndikumudziwa Earl. Earl, ine ndikukudziwa iwe, Earl Colvin. [M'bale Earl Colvin akuti, "Ine sindiri mu mzere wa pemphero, chonchobe, M'bale Bill. Ine ndamubweretsa mzathu waku Jeffersontown."—Mkonzi]. Oh, inde, eya, bamboyo pamwamba apa. Kodi ameneyo ndi mwamuna amene ife tinkasaka naye, kumtunda uko ku Colorado? ["Inu mwinamwake simungatizindikire ife, ife tachepa thupi kwambiri."] Oh, mai! Ine ndithudi sindikutero. Ine ndikukhulupirira Earl anandiuza ine kuti inu munadwala kwambiri, ndipo inu mwabwera. Tsopano, ngati inu simungathe kuyima nthawi yaitali, mulole winawake amutengere iye

mpando pamenepo. Kapena, ena a iwo—ena a iwo ayimirire ndi kumupatsa iye mpando moyandikira pomwepo, zikhala bwino, chifukwa bamboyo wadwalika kwambiri, kwambiri. Mai! Iye wataya pafupifupi mapaundi handirede kapena kuposerapo, a kulemera. Ndipo—ndipo iye—iye wadwalika kwambiri, kwambiri. Tsopano ingomulolani iye akhale pamenepo. Yambani kumuthokoza Iye pamenepo, m'bale.

225 Tsopano ndiroleni ine ndiyang'ane pansi. Tsopano, Earl anali atangoyima ndi iye. Tsopano, bambo *uyu*, wayima kumbuyo komwe uko, akundiyang'ana ine, wochokera uko kuzungulira La—LaGrange, Kentucky. Ine sindikudziwa dzina lake, koma ine—ine—ine ndikukudziwani inu. Ndipo awo ndi M'bale ndi Mlongo Kidd apo. Ine ndikuwadziwa iwo. Ndipo dona uyu, kulondola . . . Ndi Mlongo Rook ameneyo? Kapena . . . [M'bale Neville akuti, "Mlongo Hardy." Mlongo akuti, "Ndine Mlongo Taylor . . . ? . . . ndi Hattie."—Mkonzi]. Ndi mkazi uyu apa, wochokera ku Sellersburg, ine ndikukhulupirira, amene ndi wakhungu. Nkulondola uko? Chabwino.

226 Ine ndikuganiza kuti ndiwo pafupifupi onse, pa mzere, amene ine ndikuwadziwa kwenikweni. Oh, inde, apa pali mzanga wabwino, Busty Rogers, apa, wochokera kumusi ku Milltown. Ndipo mmusi pa mzere, ine ndikuganiza ena onsewo ndi alendo kwa ine. Tsopano, izo ziri pamaso pa Mulungu, monga momwe ine ndikudziwira, iwo ndi alendo kwa ine.

227 Tsopano ndiroleni ine ndiwone mwa omvetsera. Tsopano, inu—inu amene muli alendo kwa ine, amene mukudwala, mukwezere mmwamba dzanja lanu, ndipo, inu mukudziwa, muli ndi chopempha pa mtima wanu. Mukwezere mmwamba dzanja lanu, kulikonse kumene inu muli. Amene mukudziwa ine . . . Ziri bwino. Chabwino. Ndi zawamba, pozungulira, pafupifupi paliponse.

228 Tsopano, tsopano, izo sizikupwetekani inu, kungodikira utali wa mphindi imodzi kapena ziwiri. Ine ndikufuna ndikufunseni inu funso laulemu. Ine kulibwino ndipite paseri apa, ndicholinga choti inu mundimve ine. Ine ndikufuna ndingokufunsani inu chinachake. Tsopano, Mauthenga awa amene ine ndimalalikira, kodi inu mumawakhulupirira iwo kuti ndi Choonadi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Inu, ndithudi, sibwenzi mukubwera kuno ngati iwo akanakhala kuti sanali chomwecho.

229 Tsopano, kodi Mulungu angachite chinachake ngati chimenecho popanda kundipatsa ine lingaliro la chimene ine ndimachita? Iye ndithudi sangatero. Ndithudi, Iye sangatero. Tsopano, ngati Iye wachita zimenezo . . .

230 Tsopano, ine ndikunena kuti Yesu Khristu sanasinthe. Imfa yake sinamusinthe Iye; iyo inamulemekeza Iye. Ndipo Iye anawuka, tsiku lachitatu, ndipo anakwera Mmwamba.

Ndipo Iye anatumizanso Mzimu Woyera, umene unali Mulungu, ndi Mzimu Woyera umene unali pa Iye. Kodi inu nonse mukukhulupirira zimenezo? Ndipo Yesu, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anati, "Ntchito zimene Ine ndikuchita, inunso mudzazichita. Kanthawi pang'ono, ndipo *dziko* silidzandiwonanso Ine." Limenelo ndi dongosolo la dziko, inu mukudziwa, mpingo wosakhulupirira basi ndi onse. "Iwo sadzandiwonanso Ine. Komabe, inu mudzandiwona Ine." "Inu," umenewo ndi Mpingo, wokhulupirira. "Pakuti ine. . ." *Ine* ndi mlowammalo wa umwini. "Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka ku mathero a dziko lapansi." Ndipo Chigriki apo ndi *chimaliziro*, chimene chikutanthauza, "mathero a dziko lapansi." "Ndidzakhala ndi inu mpaka kumalekezero a dziko lapansi. Ndipo ntchito zimene Ine ndikuchita inunso mudzazichita." Kodi icho ndi Choonadi?

231 Tsopano, ife tiri ndi Abaptisti, Amethodisti, Achiprotestanti, ndi Akatolika, ndipo—ndipo ngakhale Achiyuda, akhala muno mmawa uno. Ndipo ife tiri ndi Church of God, Nazarene, Pilgrim Holiness, Jehovah Witness, zipembedzo zosiyanasiyana zonsezo zaimiridwa. Ine ndikuyang'ana yang'ana, ndikuwayang'ana iwo. Amethodisti, Achilutera, Achipentekoste, mitundu yonse yosiyanasiyana, pamene ine ndikuyang'ana pozungulira, kuwawona anthu amene ine ndikuwadziwa. Ndipo iwo onse ndi alendo ochokera kunja kwa tauni. Branham Tabernacle ndi kachisi wamng'ono kwambiri, kuno mu—mu mzinda, koma amapangidwa ndi anthu ochokera ku dziko lapansi.

232 Tsopano, tiyeni tingotenga ichi, ndipo tiganize mwatcheru kwenikweni, kuganiza, kuphunzira, tikhale molemekeza, ndipo tifunse funso ili. Ndiye, ngati Iye sali wakufa, ndiye maganizidwe Ake kwa inu ndi kwa odwala akanakhala omwe omwewo basi lero monga iwo analiri dzulo. Ndiyeno Iye anapanga motani maganizidwe Ake dzulo? Ichi, "Ine ndikhoza, ngati inu mukukhulupirira." Nkulondola uko? "Ngati inu mukukhulupirira."

233 Munthuyo anati, "Ambuye, tichitireni ife chifundo." Anati, "Mwana wanga wamwamuna wavutitsidwa mosiyanasiyana ndi mdierekezi. Ine ndinamubweretsa iye kwa ophunzira anu, ndipo iwo amafuula ndi kukuwa, ndi chirichonse."

234 Iye anati, "Ine ndikhoza, ngati inu mukukhulupirira. Ngati mukukhulupirira, Ine ndikhoza."

235 Tsopano zindikirani. Kodi Yesu anachita motani? Iye anali chiyani, dzulo? Iye ankatumikira chotani? Tsopano, izi ndi za kwa mlendo tsopano, ine ndikuyankhula naye. Tiyeni tiwone chimene Iye anali, dzulo. Mungonditengera ine pafupifupi maminiti atatu, tibwereza, malo aang'ono angapo.

236 Pamene utumiki Wake unayamba poyamba, pamenepo panali munthu mmodzi dzina lake Andreya, nsodzi,

anatembenuka mtima, anakhulupirira pa Iye, ndipo anapita ndipo anakamutenga m'bale wake, dzina lake Simoni. Inu mukukumbukira zimenezo? Iye anamubweretsa iye kwa Yesu. Iye anali nsodzi wosaphunzira, samatha ngakhale kulemba dzina lake lomwe. Ndipo iye anabwera pamaso pa Yesu. Ndipo Yesu anamuyang'ana iye, ndipo anati, "Dzina lako ndi Simoni. Ndiwe mwana wa Yonasi."

237 Ndi angati akudziwa kuti ilo ndi Lemba? Iwo ankadziwa kuti ameneyo anali Mesiya, chifukwa Iye ali. . .Mulungu analonjeza. Mose analonjeza, kuti, pamene Mesiya adzabwera, Iye adzakhala Mneneri. Nkulondola uko? Mneneri-Mesiya. Ndipo Iye anayang'ana, ndipo Iye anati, "Dzina lako ndi Simoni." Ndipo anati, "Atate wako anali Yonasi." Ndipo iye anadziwa kuti ameneyo anali Mesiya.

238 Mkazi pa chitsime, limenero ndi fuko lina la anthu. Tsopano, Ayuda ndi Asamariya okha anamulandira Iye. Amitundu, ife tinali tisanabwerepo apobe, gulu la Rute. Tsopano, mkazi pa chitsime, amene anali Msamaria, iye anabwera kuti adzatunge madzi. Yesu anati, "Ndibweretsere Ine akumwa." Kodi Iye anachita chiyani? Anayankhula ndi iye, basi monga momwe ine ndingayankhulire ndi winawake kunja uko mwa omvetsera. Anati, "Ndibweretsere Ine akumwa." Iwo anali asanakumanepo.

239 Ndipo iye anati, "Bwanji, si mwambo wake, ife tiri ndi tsankho kuno." Monga ankakhalira nalo Kummwera, kwa abwenzi athu achikuda ndi zinthu, koma iwo alibenso izo pano. Mathokozo akhale kwa Mulungu, chifukwa cha zimenezo. Chotero Iye anati. . . "Ife tiri ndi tsankho kuno. Bwanji, si mwambo wake kuti Inu. Inu ndi Myuda." Yesu anali Myuda. Iye anali Msamaria. Anati, "Si mwambo wake kuti—kuti Inu mundifunse ine, mkazi Wachisamaria, zimenezo."

240 Iye anati, "Koma, mkazi, ngati iwe ukanadziwa Amene iwe ukuyankhulana naye, iwe ukanandipempha Ine akumwa."

241 Zimenezo zinamuimitsa mkazi wokongola ameneyo. Ndipo iye anayang'ana mmwamba ndipo anati, "Bwanji, Inu mulibe kanthu kotungira. Chitsimecho ndi chakuya."

242 Iye anati, "Madzi amene Ine ndidzakupatsa ndi Moyo wosatha."

243 Ndipo potsiriza Iye anapeza chimene vuto lake linali. Ndi angati akudziwa, alendo, akudziwa chimene vuto lake linali? Iye anali ndi amuna faivi. Chotero kodi Iye ananena chiyani kwa iye? Iye anati, "Pita, kamutenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno."

244 Iye anamuyang'ana Iye. Iye anati, "Ndiribe mwamuna aliyense."

245 Iye anati, "Iwe wanena bwino, chifukwa iwe wakhalapo nawo faivi, ndipo amene ukukhala naye tsopano si mwamuna wako."

246 Iye anati, "Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi mneneri. Tsopano, ife tikudziwa, pamene Mesiya adzabwera," (Ameneyo ndi Yesu.) "pamene Mesiya adzabwera, Iye adzatiuza ife zinthu izi, chifukwa ife tikudziwa kuti Iye adzakhala Mneneri ameneyo. Ife tikudziwa pamene Mesiya adzabwera, Iye adzachita izi. Koma Inu ndinu Ndani?"

Iye anati, "Ine ndi Iye."

247 Ndipo pa zimenezo, iye anathamangira mu mzinda ndipo anati, "Bwerani, mudzamuwone Munthu, Amene wandiuza ine zomwe ine ndinachita: Kodi Uyu si Mesiya yemwe?"

248 Ngati icho chinali chizindikiro cha Mesiya dzulo, ndipo Iye ali yemweyo lero, ndi chinthu chomwe chomwecho lero. Tsopano, kodi inu alendo mukukhulupirira zimenezo? Tsopano, izo ndi za inu pamzere *apa*.

249 Tsopano, kwa iwo kunja uko, Lemba limodzi lokha, kuti inu mukhale ndi chinachake choti muyimepo. Ndi angati akukhulupirira kuti Iye ndi Wansembe Wamkulu tsopano, amene akhoza kukhudzidwa ndi zomverera za zofooka zathu? Ife tonse. . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . .? . . .

Atate Akumwamba, Amene mumandidziwa ine, mukudziwa, momwe ine ndikudziwira, ine sindinamuwonepo munthuyo. Tsopano iye mwina anandiwonapo ine ndipo ine mwina ndinamuwonapo iye, koma ngati izo zatero ine sindikudziwa kanthu za zimenezo. Chifukwa, ine ndazungulira dziko lapansi, kangapo, ndikupempherera odwala ndi zinthu, ndipo ine—ine mwinamwake ndinakomanapo naye kwinakwake, kapena kumuona iye, kapena chinachake, ine sindikudziwa. Koma mulimonse, ine—ine sindikudziwa chirichonse cha iye. Izo nzoona. Nkulondola uko, bwana? Basi kuti anthu adziwe. Mukuona? Chabwino. Tsopano, mwamunayo wayima pano pa chifukwa china. Tsopano kodi ali kuti mwamuna uja amene ndi mlenje, Efferson, kapena, nthawizonse-. . . Chabwino. Ndikungofuna kuti iye awone zimenezo. Izo ziri pati, Busty Rogers ali kuti? Wangoyima apo. Tsopano apa, tsopano Busty, iwe ukundidziwa ine. Bambo Efferson, inu mukundidziwa (Nkulondola uko? Efferson? Inde.), inu mukundidziwa ine, ife tinasakapo limodzi ku Colorado, ine ndi—ine ndi mwamuna. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]

250 . . . Mwamunayo akuvutika ndi vuto la manjenje. Ndiro vuto lake; chifukwa iwe uli ndi thumbo (Ndiko kulondola.), kumadzuka usiku, ndi zina zotero. Ndiwe wochokera ku Ohio. Ndipo iwe ndi wa mpingo wa M'bale Sullivan kapena umapita kumeneko. Ine ndikumuwona M'bale Sullivan wayima apa. Iwe wabwera ndi Kidds; ameneyo ndi amene wabwera naye. Uko

nkulondola. Chabwino, pa nthawi ino iwe ukumva mosiyana tsopano. Ilo lakusiya iwe. Tsopano, iwe ukhoza kupita kwanu; chikhulupiriro chako chakuchiritsa iwe. Tsopano, Mulungu akudalitse iwe.

Tsopano iwe ukukhulupirira?

251 Tsopano ine sindikukudziwani inu, bambo. Nkhope yanu ikuwoneka yodziwika kwa ine, koma tsopano, kunena za kukudziwani inu, Mulungu Kumwamba akudziwa, ine sindikudziwa kanthu za inu. Ine sindikudziwa chimene chavuta ndi inu. Ine sindingakhale ndi njira yodziwira chimene chalakwika ndi inu. Ndinu mwamuna basi amene wayima pamenepo. Ndipo inu munali ndi khadi la pemphero, pa... ilo linali ndi nambala pa ilo. Ndipo inu basi...Mnyamatayo anakupatsani inu khadi limenero, ndipo inu munangoyitanidwa kuno mu mzere wa pemphero.

252 Tsopano, tangoonani momwe izo zikubwerera. Inu mukuona, basi nthawi imodzi imeneyo, izo ndizovutirapo, izo zachita zochuluka kwa ine, nthawi imodzi imeneyo, kuposa nthawi yonse imene ine ndakhala ndikulalikira mmawa uno. Chinachake chikutuluka. Mukuona? Chinachake chikutuluka.

253 Mnyamata, iwe kwenikweni sunabwere kuno chifukwa cha iwemwini. Iwe uli pano chifukwa cha winawake, ndipo ameneyo ndi—mwana. Ndipo mwanayo sali pano; ali mu dziko losalala: Kansas. Ali ndi mtundu wina wa kugwa ngati khunyu. Khunyu ndi chimene icho chiri, pali mdima pamwamba pa mwanayo.

254 Iwe ndi wolumikizana mwinamwake, kapena, ndiwe...kwa a Strickers. Kodi inu nonse simunakwatire alongo a banja limodzi, kapena chinachake chonga icho? Uko nkulondola. Iwe ukukhulupirira? Ndiye iye sadzakhalanso ndi zakugwazo, ngati iwe uti ukhulupirire ndi mtima wako wonse. Monga iwe wakhulupirira, zikhale chomwecho kwa mwanayo. Pita tsopano ndipo usakaikire zimenezo.

Tsopano inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Anthu nonsenu? Mukumupempherera winawake. Pempherani ndipo musiyeni Mulungu apereke.

255 Dona uyo wakhala apoyo, akuwapempherera azakhali amenewo, ali ndi khansa; pansi mmenemo. Iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse, kumbuyo uko, iwe ukutero? Ine sindikukudziwa iwe. Ine sindinakuwonepo mmoyo wanga. Koma pamene iwe unandimva ine ndikumuuza mwamuna uyo za chinachake chimene iye amachiganizira, cha wachibale, icho chinabwera kwa iwe. Tsopano, iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse?

256 Tsopano, kodi iye wakhudza chiyani? Ine ndikufuna ena a anthu inu, mundiuze ine chimene mkazi ameneyo wakhudza. Iye ali mapazi twente kuchoka kwa ine iye sanandikhudze ine, koma iye anakhudza Wansembe Wamkulu ameneyo. Iwe ukuwona,

Busty? Inu mukuona, bwana? Iye anakhudza Khristu. Khristu anabwera pano ndipo anadzandiuza chimene iye amafuna, tsopano iye wapeza chimene anachipempha.

Mkazi, ine sindikumudziwa mkazi uyu. Iye ndi mlendo kwa ine. Nkulondola uko? Ndife alendo. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga monga ine ndikudziwira, koma Mulungu akumudziwa iye. Ngati Mulungu angandiuze ine chinachake cha iwe monga Iye anachitira ndi mkazi pa chitsime, kuwulula chinachake chimene chiri mu mtima mwako, kodi iwe uvomereza icho, ndi kukhulupirira kuti sizingakhale ine, monga munthu, ndikukuuza iwe zimenezo, zimenezo zingakhale—zimenezo zingakhale Mulungu? Iwe ungakhulupirire izo?

257 (Tsopano, kodi uyu ndi thuu, kapena ndi angati awa? Ife tinali kale ndi firii? Thuu? Thuu? Chabwino. Chabwino.)

258 Donayo ali ndi mthunzi wa imfa. Pali mthunzi wakuda pa iye, umene iye ali ndi khansa. Uko nkulondola. Dokotala wakuuzani inu kuti iyo ndi khansa ya mmitsempha. Uko nkulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndinu wochokera kutali ndi kuno: Iowa. Inu mukukhulupirira? Inu muli ndi, mwina mwana wamwamuna, kapena, ndi mdzukulu wamwamuna, ndipo ali ndi chinachake cholakwika ndi maso ake, ndipo inu mukumupempherera iye. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu angathe kundiuza ine kuti inu ndi ndani? Akazi a McKee, ndiye mubwerere kwanu, ndipo mukakhale bwino. Yesu Khristu wakuchizani inu.

Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse tsopano? Ine sindinamuwonepo mkaziyo mmoyo wanga. Chimachita izo ndi chiyani?

259 Mphindi chabe. Molemekeza, mphindi chabe. Ine ndikuyang'ana pa mkazi wachikuda wakhala kumbuyo komwe kuno kumbuyo; ndipo Kuwala kuja, kumene inu mumakuwona pa chithunzi chija, kwapachikika pa mkazi ameneyo amene wakhala kumbuyo uko. Mundikhulupirire ine kuti ndine mneneri Wake, mlongo. Inu mukupempherera mwamuna wanu ali wakuti akhoza kufa ku Veterans Hospital; ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse tsopano; iye akhala bwino.

Kodi iye anakhudza chiyani? Apo pali mkaziyo, mkazi wachikuda, mwamuna wachizungu, monga mkazi pa chitsime. Kodi iye anakhudza chiyani? Yesu yemweyo. Iye si mkazi yemweyo, mkazi wachikudayo anali, kapena, mkazi Wachisamaria anali; ndi mkazi wina. Ine si Yesu, munthu yemweyo; Ndine munthu wina. Koma iye ndi wokhulupirira pa Yesu Khristu, monga mkaziyo anali; ndipo ndine wokhulupirira ndi wantchito Wake, ndi Mzimu womwewo ukugwira ntchito mu tsiku lino. Khristu sanafe, Iye ndi wamoyo. Ine sindinamuwonepo iye kapena kumudziwa iye mmoyo wanga.

Tsopano, inu mwaona, inu simukuyenera kuti muchite kukhala ndi khadi la pemphero kuti mukhale pano. Inu mungokhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Si kulondola uko?

260 Tsopano ine ndikumudziwa mkazi ameneyo pamenepo, koma ine ndikudziwa chimene iye akupempherera: mdzukulu wamkazi ameneyo. Inu mukukhulupirira zimenezo (kumusi kummwera), ngati inu mungakhulupirire ndi mtima wanu wonse, iye akhala bwino.

Nanga bwanji inu? Ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ndinu mnyamata chabe. Ine sindinakuwonenipo mmoyo wanga. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu angathe kundiuza ine chimene vuto lanu liri? Ngati Iye atatero, zimenezo zikuthandizani inu? Ndithudi.

Tsopano, basi, inu muzingokhulupirira kunja uko. Mukuona?

261 Vutolo liri pa khosi panu. Inu munachita ngozi ya galimoto. Inu mwabwera kuchokera kumpoto. Muli pafupi ndi Bedford, Indiana. Izo nzoona. Kodi izo nzoona? Ndiye inu—inu mukukhulupirira kuti khosi lanu likhala bwino bwino? Pamene mukukhulupirira, zikhale chomwecho kwa inu. Bwererani kwanu ndipo muzilemekeza Mulungu. Muchiritsidwe.

Muli bwanji, bwana? Inu mukukhulupirira kuti Mulungu angathe kuulula kwa ine vuto lanu? Inu mukuvutika ndi a—chochitika cha manjenje; zinakupangitsani inu kukhala ndi vuto la matumbo, thumbo, vuto la matumbo. Ndinu ochokeradi ku California. Uko nkulondola. Inu mukukhulupirira Mulungu akudziwa yemwe inu muli? Bambo Murray? Chabwino, ilo latha tsopano. Bwererani kwanu; mumukhulupirire Iye ndi mtima wanu wonse.

Kodi ndife alendo kwa wina ndi mzake? Ine sindikukudziwani inu, ndipo Mulungu. . . Ine sindikukudziwani inu ndipo inu simukundidziwa ine. Ndife alendo, nkulondola uko? Ngati Mulungu ati awulule kwa ine chinachake chokhudza inu, kodi inu mundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake?

Kodi ena nonsenu mukhulupirira? Ine ndi. . . Izo zikundipangitsa ine kufooka kwenikweni, kufooka tsopano, mwaona. Mungokhulupirira tsopano. Ndine basi. . . Kudzoza kuli pano. Inu mukudziwa zimenezo, sichoncho inu? Ndinu—mukudziwa kuti iko—iko kuli pano, mwaona. Mzimu Woyera uli pano tsopano ngati inu mungathe basi. . . Ine ndikufooka kwambiri moti ndikulephera kuti ndikuwoneni inu kenanso kunja uko. Mukuona? Inu. . . Ngati chochitika chimodzi chinamupangitsa Yesu kufooka, kodi seveni kapena eyiti zingatani, zochitika teni, ife takhala nazo, pano, kudzera mwa omvetsera? Faivi kapena sikisi kapena seveni kunja kuno pa nsanja ndi firii, kapena foro, kapena faivi, kunja uko. Mukuona? Zangondifikitsa ine pamalo amene sindingathe

kuwonanso. Zikuwoneka kuti gulu lonse la anthu likukhala ngati mkaka. Ngati mutangozindikira kuti ndiko kuchulukitsa kwa Mzimu Woyera ukusunthira mkati. Ndi Kuwala kuja, apo, kukuyandama pamwamba pa chipindachi. Mwaona, Ndizo, Iye akukubweretsani inu mu kuwundana, pa malo.

Tsopano, pokhala kuti mkazi uyu wayima apa, kwa inu mu mzere wa pemphero tsopano: Ngati Mulungu ati awulule (Apa, ine ndakweza manja anga mmwamba, ine sindinamuwonepo mkaziyo, sindikudziwa kanthu za iye.), ngati Mulungu ati awulule ndendende, kulola, chimene iye wachita, kapena chimene iye ali, kapena, chabwino, chinachake chimzake cha iye, kodi nonse a inu mukhulupirira, ndiye, kuti ndizo, Mulungu akuchita zimenezo? Kodi inu mukhulupirira izo? Ndipo kodi inu mukhoza—mukhoza kuvomereza? Kodi inu mukhulupirira kuti mukhala moyo tsopano? Kodi inu . . . Chifukwa ndikudziwa vuto lanu, ndikudziwa vuto lanu, lanu, silinabisike. Inu mukuona? Mulungu amaulula zinthu zimenezo, koma ngati inu mutangokhulupirira.

Tsopano, ine ndibwera ndi kudzaika manja pa inu chifukwa ine ndikuyamba kufooka kwenikweni, kwenikweni. Ndipo ine ndikudziwa mu kamphindi, chabwino, ine—ine sindimatha kuwonanso, mwaona.

262 Tsopano, inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Tsopano kumbukirani, si ineyo. Aliyense akudziwa zimenezo. Ndi Mzimu Woyera. Uh-huh. Tsopano, ngati nditangowugwira mzimu wa mkaziyo. Ndicho chinthu chomwecho chimene Yesu anachita. Akuyesera kuti awugwire mzimu wake, Iye anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.”

Apa pali mwamuna ndi mkazi, monga momwe zinaliri kumeneko. Tsopano, ndiwe mkazi wamng’ono, wocheperapo kwambiri kuposa ine. Tsopano, mwinamwake, mwina mkazi uyu anali wamng’ono kwa Yesu. Iye anali pafupifupi ndi zaka sarte-firii; ndipo mwinamwake mkaziyo sanali koma eyitini kapena twente, mkazi wamng’ono chabe. Ndipo iye—iye—iye amalephera nkomwe kudziwa choti anene koma pamene Iye anadzayankhula ndi iye Iye anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.”

Tsopano Atate anali atamutumiza Iye ku Samaria. Iye anali pa ulendo Wake waku Yeriko, koma Iye anapita mozungulira Samaria; uko ndi pamwamba pa phiri. Nchifukwa chiyani Iye anachita zimenezo? Iye anati Iye anali ndi chosowa choti adutsireko. Atate anamutumiza Iye kumeneko. Chabwino, Iye anangobwera ndi kudzakhala pansi, ndipo anawatumiza ophunzira mu mzinda kuti akagule chinachake choti adye. Ndipo mtsikana wokongola uyu anabwera kudzatunga madzi, ndipo Atate akuyenera kuti anati, “Ndikuitanira iye.”

Iye anati, “Mkazi, ndibweretsere Ine akumwa.” Ndipo kuchezako kunayambika. Tsopano, chinthu chomwecho apa.

Kodi munayika dzanja lanu pa chikhothi changa? Mmodzi wa inu? Ayi bwana. Mulungu Kumwamba akudziwa Chinachake chinandikhudza ine pamenepo, pamene . . . Ine ndimaganiza kuti anali Billy akundiuza ine kuti ndichokepo. Mwaona. Ine—ine—manja anga, Mulungu akudziwa kuti zimenezo nzoona. Chinachake chinandikhudza ine monga choncho ndipo ine ndimaganiza kuti ndi Billy akundiuza ine, "Zipitani." Mwaona, ine—pamene ufika monga chonchi, iwe sumadziwa nkomwe, iwe sumadziwa kuti uyimire pati kapena choti uchite. Inu mukuona? Iwe umangokhala pambali pa iwemwini. Kodi ine ndimakamba za chiyani? Mkazi pa chitsime.

Ndipo kenako Iye atapeza pamene vuto lake linali, ndipo Iye anati, "Pita, ukamtenge mwamuna wako."

Iye anati, "Ine ndiribe." Ndipo Iye anamuuza iye, anati iye anali nawo faivi.

Kenako iye anati, "Ine ndazindikira kuti Inu ndi mneneri. Ine ndikudziwa pamene Mesiya adzabwera, Iye adzatiuza ife zinthu zimenezi."

Tsopano kodi uyo angakhale Mesiya yemweyo lero, ngati ine ndingakuuze iwe chinachake, chinachake chimene chiri cholakwika? Ngati Mulungu sakuthandiza iwe, iwe ufa. Iwe uli ndi khansa. Tsopano, iwe ukukhulupirira Mulungu akhoza kundiuza ine pamene khansa imeneyo ili? Iyo ili mu chiberekero. Iwe ukukhulupirira Mulungu akudziwa kuti ndiwe ndani? Iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akudziwa kumene iwe ukuchokera? Ndiwe wochokera ku Illinois. Ndiwe—dzina lako ndi Abiti Johnson. Bwerera ndipo ukakhale moyo. Yesu Khristu wakuchiza iwe. Iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse? Basi . . . Msiyeni iye akhale moyo . . . ? . . . Pali chifukwa chimene ndakuuzira iwe kuti ukhale moyo.

Atate Kumwamba, mu Dzina la Ambuye Yesu, ine ndikusanjika manja anga pa mkaziyu tsopano; kudzoza kwa Mzimu Woyera kuli pano. Mchiritseni iye, Ambuye, mu Dzina la Khristu, Yesu.

Wokondedwa Mulungu, pa m'bale wathu wofunika, amene Inu munapulumutsa moyo wake kumbuyo uko, mu Ogasti, O Mulungu wachifundo, bwerani kwa iye tsopano, pamene Mzimu Woyera ukudzoza mitima yathu. Ine ndikudziwa mayesero a m'bale wanga. Mchizeni iye, Ambuye, ndipo mumupange iye akhale wabwino . . . ? . . .

Iwe unali ndi vuto la mtima, iwe uli ndi matenda a shuga; ine ndikudziwa kuti ukuvutika, chonchobe, ndizo . . . ? . . .

Atate Athu Akumwamba, mwamuna uyu ali . . . ? . . . iye akuyenera kukupezani Inu kapena afa. Iye amakonda kupita kuchipatala . . . ? . . . Mukhululukireni machimo ake ndipo muchiritse thupi lake mu Dzina la Yesu Khristu mulole iye akhale moyo. Kazipitani kwanu, zipitani.

Chabwino, apa, inu nonse mumutengere m'bale uyu kwanu.

Mulungu wathu wofunika, mu Dzina la Yesu Khristu, manja anga ali pa iye pamene kudzoza kwa Mzimu Woyera kuli pafupi. Mulole anthu azindikire izo. Mulole iye achiritsidwe.

Atate Mulungu, pamene ine ndikuyika manja anga (manja anga, thupi langa losayenera, lachivundi, lovunda ndi loipa; koma Mzimu Woyera uli pa ine tsopano), mulole mphamvu imene ikhoza kuzindikira malingaliro a mtima imusamalire mkazi uyu ndi kuchiritsa thupi lake, mu Dzina la Yesu.

Wokondedwa Mulungu, pomudziwa m'bale wanga ndi chikhalidwe chake, podziwa kuti cholepheretsa kuyankhula ichi . . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

O Mulungu, za mnyamata uyu, akumenya nkhondo yabwino ya chikhulupiriro, wayima mu Kukhalapo kwa Yehova-Yire, Nsembe yoperekedwa ndi Ambuye, mulole mphamvu imene inamuwukitsa Yesu mmanda, imukhudze iye pakali pano. Mpatseni iye chokhumba cha mtima wake, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

263 Ambuye Yesu, pa mlongo wanga ine ndikuyika manja anga. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole maso awo akhale bwino. Mulole iye—kusautsika kwake kuchoke pa thupi lake, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

264 Atate Athu Akumwamba, chifukwa cha Mlongo Kidd wanga wamng'ono, ine ndikupemphera kuti Inu mugonjetse mwa iye, ndi kumupatsa iye mphamvu mu ukalamba wake monga Inu munachitira ndi Naomi. Ambuye, mulole iye agwiritsidwebe ntchito kwa ulemelero Wanu. Perekani izi, Atate, mu Dzina la Yesu Khristu.

265 Kenako kwa M'bale Kidd, Ambuye, imfa imeneyo inamukantha iye, koma Moyo unamubweretsanso iye. Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mumusunge iye wamphamvu. Iye wadutsa nthawi yake imene anapatsidwa. Koma Inu ndi Mulungu, ndipo Inu muchita izi kwa ulemelero Wanu monga Inu munandilonjezera ine mu chipatala. Tsopano, mpatseni iye mphamvu chifukwa cha umboni. Mulole umboni wake umveke kudutsa mu dera la Ohio, mu dziko lonse. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

Kuti Yesu akundichiritsa ine tsopano.
Ine ndimutenga Iye pa Mawu Ake . . .

60-1002 Muwomboli Wachibale
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org